


MKWATULO

 . . . Yuma. Ndi mwayi wawukulu kukhala ndi kuyitanidwa uku kuti ndibwererense. Ife tinali ndi nthawi yopambana nthawi yapitayo kuno, ndiyeno ine—pamene ine ndinadziwa kuti ndibwereranso, zinandipangitsa ine kumva bwino zedi. Kumva maumboni ndi mawu awa abwino kuchokera kwa anthu, ndi zokhoza kukukweza iwe pang'ono.

² Billy anandiwuzwa ine kuti m'bale wochokera ku Las Vegas amene ankafuna msonkhano kumeneko pa msonkhano wapadera, ndimuwone iye ukangotha msonkhanowu pano. Ife tiri ndi nthawi, iye akutero, kuti ife tikhoza kuchokapo mu Januwale msonkhano wa ku Pheonix usanachitike (mwaona?) kuti tibwere ku—ku Las Vegas. Ndipo kotero ife nthawizonse tafuna titapita kumeneko. Ine ndikukhulupirira M'bale Art Wilson ankakhala kumeneko nthawi yakale, kapena iye mwina adakali komweko. Ndipo iye—iye anandifunsa ine kuti ndidzapiteko, iye ndi Mlongo Wilson. Ndipo ine sindinapeze danga, kotero mwina ino idzakhala nthawi yoti ine ndikanakhoza kubwera.

³ Inu mumuwone Billy Paul kapena M'bale Roy Borders—ine ndikuganiza kuti iye ali muno penapake. Wina anati M'bale Roy anali muno—M'bale Pearry, Lee, kapena aliyense wa iwo, iwo akhoza kukuwuzani inu, ndipo ingotipangirani tsiku loti tidzabwere.

⁴ Tsopano, ine ndinawona alaliki ambiri pano kanthawi kapitako chomwe ndakondwera kwambiri kukumana ndi abale anga. Ndinangokhumba ndikanakhala ndi nthawi. . . kupita nanu kunyumba, chifukwa ine ndikudziwa kuti inu muli ndi wodziwa kuphika kwambiri yemwe alipo mu dziko lonseli. Izo nzabwino. Ndipo ine. . .

⁵ M'bale Pearry anadzipezera mayamikiro awiri madzulo ano. Iye ali ndi ziwiri zomutsutsa iye tsopano: chimodzi mwa izo ndicho kudula maikolofoni awo kunjako. Inu muli—mwapezedwa olakwa pa icho, M'bale Pearry. Ine sindikuganiza kuti inu munalakwitsadi, koma inu. . . “Wina amafuna kulankhula.” Umenewo unali wabwino.

⁶ Ndipo kotero, ndiyenso iye anapita kunjako ndipo anali kulankhula; iye anati, “Nnena. . .” Iye amamuwuzwa M'bale Collins kapena ena mwa iwo, anati, “Chakudya cha madzulo chinali chabwino, koma,” anati, “Ine ndikukuwuzani inu,” iye anati, “bambo amene uja ayenera kukhala wachi Spaniard, kapena chinachake, kapena wachi Mexico. Amene uja anali tsabola wowawa kwambiri amene ine sindinayambe

ndamulawapo!” Kumapitiriza chotero; ndipo iye nkuti akulankhula ndi mkulu wa zophika.

Iye anati, “Ndine mkulu wa zophika.”

⁷ Ameneyo ndi wachi Texas kwa inu. Ife timuwongola iye bwino kuno mu Arizona pakapita kanthawi sichoncho ngati iye ati akhale pafupi—nafe?

⁸ Ndi bwino zedi kukhala pano. Ndipo ndikuganiza kuti izo sizikumveka ngati nthabwala, koma khalidwe losangalatsa. Limene Ambuye Mwiniwake anali ndi khalidwe losangalatsa, inu mukudziwa. Iye anati “Herodi . . . pita ukayiwuze nkhandweyo. (Mwaona?) Lero ine nditulutsa—sinditulutsanso ziwanda konse . . . Ine ndapangidwa kukhala wangwiro.” Kotero ngati Iye anali—anali ndi khalidwe losangalatsa, bwanji, sizitipwetekanso ifeyo, ine sindikuganiza, kamodzi mu kanthawi.

⁹ Ndipo tsopano, ndi—tachedwa pang’ono. Ndipo nthawizonse ine—ndimalalikira pafupi maora anayi. Kotero pongodziwa za ulemu wa m’bale ndi mlongo wa msonkhano wapaderawu kuno, tidula pang’ono pamenepo usiku uno. Ndipo Inde, ine ndinamuwuza Terry, ine ndinati . . . Iye anati, “Ndi chiyani . . . Ife tinayika tepi ya maora awiri?”

¹⁰ Ine ndinati, “Ayi, Terry; ili ndi—phwando.” Ine ndinati, “Maminiti pafupi makumi atatu, makumi anayi chabe, kulankhula kwa anthu pa—a chinachake chimene . . . Ndikhoza kuyesa ngakhale nthawi iliyonse, podziwa kuti . . .”

¹¹ Pamene ine ndinali kamnyamata kakang’ono, ine—anthu anakonda kubwera kudzamvera chifukwa chakuti ine ndinali—mlaliki wachinyamata, kamnyamata chabe, kamwana. Ndipo iwo amakhoza kunena, “Chabwino, Billy Branham . . .” Inu mukudziwa, mwana chabe, osadziwa—anangodusako ku sukulu ndi wopanda maphunziro. Ndipo iwo amakhoza kubwera kudzamvera mawu anga othyokathyoka, Chizungu changa cha ku Kentucky. Ndipo—ndipo kotero iwo—ndi ma *hit’s*, ndi ma *haint’s* anga, ndi ma *totes* ndi ma *carry*. Monga umodzi wa misonkhano kuno posachedwapa iwo anati, “Ife tonse tiyima ndi kuyimba Nyimbo ya Fuko.”

¹² Ine ndinayimirira ndikuti “Pakuti kwathu kwakale ndi ku Kentucky kutali.” Ilo linali fuko lokhalo lomwe ine ndinkalidziwa, kotero iyo inali Nyimbo ya Fuko momwe ine ndimakhudzidwira.

¹³ Kotero tsopano, mutakula pang’onobe, bwanji, ife—inu mukabweramo, inu muyenera kukhala ndi chinachake choposa icho. Mukuona, ife tikutenga . . . Paulo anati kuti, “Pamene ine ndinali mwana, ine ndinkalankhula ngati mwana ndi kuganiza ngati mwana.” Inu mumachita ngati mwana, koma pamene inu mukulirapo, ndiye inu mumayamba ku—kuyambira pakuyenda masitepe anu angapo oyamba ndi kuterereka ndi kugwa, ndi

kudzukapo ndi kuyesanso. Ndiyeno inu—patapita kanthawi inu mumafika pakuti mungayende mzere wolunjika. Ndipo ndizo zomwe ife tiyenera kuchita monga asirikali a mtanda; tsopano ndi nthawi yoyenda mzere wolunjika mu msewu waukulu wa ku ulemerero.

¹⁴ Ine ndikukhulupirira kuti ife tikukhala mu nthawi ya kutseka kwa zochitika za mbiriyakale ya mdziko ili. Ine ndikukhulupirira moona kuti kudza kwa Ambuye kwayandikira mwina kusiyana ndi momwe ife tikuganizira. Kotero tsopano, kwa maminiti pafupi makumi atatu okha a nthawi yanu kapena chinachake, ine ndikufuna nonse mukhale tcheru ku Malemba amene ine ndikufuna kuwagwiritsa ntchito kwa—phunziro ndi—powerenga mogwirizanitsa kwa ena ochulukira apa. Ine...Nditakhala kunyumba tsiku lina, ine ndinali kuganizira pa lingaliro ili. Ndiye ine ndinaganiza, “Chabwino, ine sindikudziwa, kulankhula kuchokera pa Malembo onsewa, ine ndingotenga gawo lake ndipo kwa misonkhano yaifupiyi monga momwe ife tingafunire kukhala nayo usiku uno. Ine ndikufuna kunena chinthu chimodzi pamene inu mukutsegula mu Masalimo—yoyamba, Salimo la 27, ine ndikufuna ndime zisanu zoyambazo kuti ndiwerenge.

¹⁵ Ndikanafuna kulankhula ichi pokhudza misonkhano iyi ya Anthu Amalonda—misonkhano yapadera ya Full Gospel Business Man. M'bale wanga Pearry anali kulankhula za mabuku ndi zina zotero, ndi mabuku atsopano amene iwo ali nawo. Ndi angati amene akukumbukira pamene ife—ine ndinali ndi tepi ndipo inali—ndinalalikira iyo kuno ku Pheonix, pa umodzi mwa misonkhanoyi ya *Mabwana, Kodi ndi Nthawi Yanji Iyi?* Tsopano, uko kunali kuyamba kwake kwa bukhulo (mukuona?) pamene—izi zinachitika.

¹⁶ Pali kutsimikizira kwauzimu kochuluka kwa Mawu olembedwa a Mulungu a ora lino kuti chinachake chisakhale chikutiyandikira ife tsopano. Ife tangokhala—ndi zenizenidi. Onani, zinthu zimene inu...Zingakhale zodabwitsa kwa inu kungokudziwitsani inu kuti—zomwe zikuchitika kwenikweni. Ambiri a inu alendo mwina mwawamvapo anthu awa akunyamuka napanga—kupanga ndemanga izi za Uthenga wa ora lino ndi zina zotero. Chimene iwo akunena, ndi lonjezo la Mulungu la ora lino, limene Iye analonjeza la zomwe Iye ati adzachite, ndipo ife tikumuwona Iye akukwaniritsa Mwamalembo chimodzimidzi zomwe Iye anati adzachita mwa njira yomweyo. Zoneredweratu, zikungodzachitika momwemo, mwangwirowo nthawi iliyonse, chifukwa ndi Mulungu amene wazinena izo.

¹⁷ Ngati munthu, ine sindikusamala kuti ndi ndani, atayesa kulosera chotero...Pali mwayi umodzi pa mamiliyoni khumi ngati munthu atakuwuzani inu chinthu chinachake kuti chidzachitika, chidzatero—chidzachitika panthawi yina,

kamodzi pa ka miliyoni khumi. Ndiyeno pamalo pomwe zikanati zidzachitikire akhodza kudzakhala mwina mwa mwayi umodzi pa mamiliyoni zana. Ndiyeno, nthawi yomwe zingadzachitike, kupitirirapitirira. Ndi njira yomwe ziti zidzachitikire ndi chomwe chiti chizidzachitika ndi zina zotero, ndi zopyola kungoganzira. Pamene ife tikuwona izo zangwiwo chotero kamodzi ndi nthawi iliyonse, ndiye ndi Mulungu. Izo . . . Ndiye ife tikubwerera mu Malemba—zikhoza kuwoneka zachilendo kwa ife, koma ife tikubwerera mu Malemba popanda ngakhale kudziwa koti nkuyang'ana, ndipo Mzimu Woyera umazibweretsa ndi kungoziyika mu Mawu onse palimodzi, zimapanga chithunzi pamenepo chotisonyeza ife ora limene ife tikukhalamo. Ife tikusinthana nyengo.

¹⁸ Ife tiri—tiri pa ngodya. Ndi zophweka pamene wina akhota ngodya—womanga nyumba—akakhotetsa ngodya nayamba. . . Aliyense nkumayala njerwa pa mzere womwewo, monga momwe chipembedzo china chimayambira ndi kuyamba kupitirira mu mzere, izo nzabwino; koma pamene inu mufika pa malo okhota awo pamene inu muyenera kukhota mu njira yina. . . Tsopano, Mulungu sakumanga khoma ayi; Iye akumanga nyumba. Mwaona? Ndipo pali modutsa mwambiri ndi mokhota izo Iye ananeneratu mu Baibulo umu. Ndipo ndi mokhotamo. . . Aliyense akhoza kuyesa kukhota, koma ziyenera kukhala molingana ndi pulani. Ngati sizitero, iyenera kuphwasulidwanso.

¹⁹ Kotero ife—ife timayamika Mulungu chifukwa cha ubwino Wake ndi chiyanjano cha inu anthu, ndi makomo otseguka amene Ambuye atipatsa ife. Ndipo kupyolera mwa Anthu a Amalonda awa. . . Ine nthawizonse ndakondwera kuti ine—ine sindinakhulupirire mu. . . ine ndimakhulupirira mwa anthu mu zipembedzo, koma ine ndiribe nthawi yokwanira kuti ndiyamikire zipembedzo, chifukwa aliyense amadzimangira mpanda modzizungulira yekha, ndipo. . .

²⁰ Ndipo zangokhala monga ngati ndi. . . Ine ndikukhulupirira kuti ndi M'bale David kamwambi kawo, ka momwe iye ankawetera abakha, ndipo anati, mtsinje unadzaza ndipo bakha aliyense, inu mukudziwa, kuti amafuna chiyanjano wina ndi mzake ndipo iwo samakhoza kutero chifukwa iwo onse anali otchingidwa ndi mipanda. Koma pamene madzi anakwera kwambiri, iwo anangoyandamitsa abakhawo kupita kunja kwa kholalo. Kotero ine—ine ndikuganiza kuti umu ndi momwe ziyenera kuchitikira. Ndi kungo. . . Madzi kukwera (mukuona?), ndipo ife tikhoza kutuluka mu khola ndi—ndi kuyanjana wina ndi mzake, inu mukudziwa, kukhala ndi chikondi chenicheni cha Khristu mu mtima wathu.

²¹ Ndipo awa a Full Gospel Business Men akhala—kachitsime kwa ine, chifukwa nthawi zambiri ine ndiri ndi abale, abale abwino, m'menemo, ine ndikuganiza, mpingo uliwonse womwe

ine ndakomana nawo, Apresbateria, Aluterani, Abaptisti, Achipentekoste, a—mitundu yonse ya Chipentekoste, Church of God, ndi Anazareni, a Pilgrim Holiness, abale abwino kulikonse. . . Koma nthawi zambiri iwo sangakhale nane mmidzi yawo, chifukwa. . . Mwaona? Osati kuti sakukhulupirira izo, koma onani, zingawachotsetse iwo ku chipembedzo chawo. Ndipo pamene inu muchita icho, chifukwa izo—izo zimachita icho.

²² Kuno posachedwapa kunali m'bale wa Methodisti amene anadza kwa ine. Ine sinditchula dzina lake, bambo wabwino. Iye anali akulemba lingaliro pa za Machiritso Azuzimu, ndipo iye anadza kwa ine chifukwa cha zina—kuti adzalankhule nane. Iye tinakhala pansu ndi kulankhulana kwa kanthawi. Ndipo iye anati, “Chinthu chokha chomwe ife tiri nacho motsutsana nanu, inu mukumakhala pakati pa anthu Achipentekoste nthawizonse.”

Ine ndinati, “Ndiyetu a Mpingo wa Methodisti azikonza iyo; ine ndibwera.”

Izo zinali zosiyana. Mwaona? Iye—iye anati, “Chabwino, ndithudi ine—ine si mpingo wa Methodisti; ine ndangokhala wa iwo.”

²³ Ine ndinati, “Ndi zimenezotu!” Mwaona? “Iwo ndi amene, Achipentekoste ndi amene amatsegula khomo lawo.” Mwaona? “Ndiwo omwe ine ndingafike kwa iwo.” Ndi ena ambiri omwe ati adzatsegule, bwanji, ife tiri okonzeka kudzalowamo. Monga mu Chivumbulutso mutu wa 3 Iye anati, “Ine ndayima pakhomo ndikugogoda. Ngati munthu aliyense adzatsegula khomo, ine ndidzalowamo ndi kudya.” Ndipo uyo anali Yesu. Ine nthawizonse ndimadziwa kuti uyo anali Khristu. Ndipo Iye ndi Mawu. Izo nzolondola! Iye ndi Mawu.

²⁴ Ndipo kotero a Full Gospel Business Men akhala chitsime komwe ife tingabwere palimodzi. Palibe mpingo womwe ukulipirira uwu. Iwo palimodzi, anthu a mmpingo, ndipo ife timadza palimodzi mchijanano mdziko lonse, kuzungulira, kulikonse.

²⁵ Ndipo ine ndathandiza kukhazikitsa ambiri, ambiri, magulu ambiri mu dziko lonseli a Full Gospel Business Men. Ine ndikuthokoza chifukwa cha mwayi umenewo umene unapatsidwa kwa ine. Mmenemo a Business Men amalipirira iyo, ndiyeno mipingo yonse, iwo—iwo akufuna kubwera basi. Koma ndiye ngati. . . ine sindikufuna kumayesa kuwakoka anthu kuchokera ku mipingo yawo. Ingokhalani mu mpingo wanu nkumamwaza Kuwala. Mwaona? Khalani Mkristu weniweni; abusa anu akuyamikirani inu. Woyera weniweni, wodzipereka, wowona mtima, munthu aliyense amene amakhulupirira mwa Mulungu adzayamikira munthu wotereyo. Inde!

26 Tsopano, ine ndikuthokoza m'bale pano ndi mkazi wake ndi gulu lino chifukwa cha mwayi uwu. Ndipo gulu limeneli litakula; madalitso a Mulungu atakhala pa ilo, ndipo likhale chida m'dzanja la Mulungu kuti likapululumutse mazana mazana a anthu Ambuye asanadze. Ndipo ena nonsenu a magulu inu—kapena oyimira ake pano kuchokera ku magulu ena . . .

27 Mu Bukhu la Masalimo . . . Tsopano, ine ndikufuna kulankhula pa—phunziro lachirendo lenileni usiku uno kwa kanthawi pang'ono. Ine ndiri ndi Malembo ena olembedwa apa, ndipo—ndipo ine ndimaganiza kuti mwina . . . Usiku uno ndimati ndilankhule pa chinachake chosiyana, koma powona nthawi ikutha, bwanji, ine sindinafune kuti ndikhale nthawi yaitali chotero, kotero ine ndinangotembenezira apa ndikupeza Malembo ena ambiri. Ndipo ine ndikufuna kulankhula pa phunziro la *Mkwatulo*. Mwaona?

28 Tsopano, ife tikukhulupirira kuti kudzakhala mkwatulo. Akhristu onse amakhulupirira izo, ndiwo owerenga Baibulo omwe amakhulupirira kuti kudzakhala mkwatulo.

29 Ndipo tsopano, kuwerenga kuti—tipange maziko, ife tiwerenge Masalimo 25—ine ndikutanthawuza—pepani—Salimo la 27, ndime 1 mpaka 5.

AMBUYE ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa; ndidzawopa yani? AMBUYE ndiye mphamvu ya moyo wanga; ndidzachita mantha ndi yani?

Pamene oyipa, ngakhale adani anga omwe ndi azondi anga, anadza pa ine kudzadya mnofu wanga, iwo amapunthwa nagwa.

Ngakhale gulu la ankhondo lindizinga pafupi nane, mtima wanga siwudzawopa: ngakhale nkondo indiwukire ine, mmenemo ine ndidzakhala ndi chidaliro.

Chinthu chimodzi ine ndinachipempha kwa AMBUYE, kuti ndichifunefune; ndicho kuti ndikhale mnyumba ya AMBUYE masiku onse a moyo wanga, kupenya kukongola kwa AMBUYE, ndi kumafunsa mu kachisi wake.

Pakuti mu nthawi ya masawutso iye adzandibisa ine mu hema: ndi mu malo obisika a kachisi wake Iye adzandibisa ine; iye adzandikhazika ine . . . pa thanthwe."

Ambuye awonjezere madalitso awo pa kuwerenga uko kwa Mawu Ake.

30 Tsopano lero, kulankhula pa phunziro ili . . . Ndipo tsopano, ena a inu mukhoza kusiyana nane—njira zomwe ine ndikuzitenga, koma ndi angati muno amene akukhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa kuti kudzakhala mkwatulo wa

Mpingo? (inde, bwana! Izo nzolondola!...?....), kutengedwa kwa mpingo. Kaya ndinu wa Methodisti, Baptisti, Presbateria, kapena chirichonse chomwe muli, Achipentekoste, padzakhala kutengedwera kwina.

³¹ Ndipo ine ndikuganiza kuti polankhula ine—ine sindimangobwera pano ndi kulankhula chinachake chomwe ndikuganiza kuti chiwasangalatsa anthu. Ine sindinakhalepo ndi mlandu woterowo. Ine ndimafuna kufika pano ndi kulankhula chinachake monga ndikuwonera kutsogoleredwa kuti ndichilankhule, chimene ine ndikuganiza kuti chingakhale thandizo kwa inu, chinachake chimene chingapitirize zokuchitikirani zanu ndi Mulungu ngati inu muli Mkhristu, ndipo ngati simuli Mkhristu, kukuchititsani inu kuti mudzimvere manyazi nokha mwakuti inu mudzakhale Mkhristu. Ndipo ndicho cholinga chomwe ine nthawizonse ndayesetsera kulondoleza malingaliro anga momwe Ambuye anganditsogolere ine.

³² Tsopano, ife tachenjezedwa, monga mu chiphunzitso cha ichi mu masiku otsiriza chidzanyozedwa. Ngati inu muta... Tiyeni tingowerenga izo kwa miniti yokha. Ndi mu 2 Petro mutu wa 3. Tiyeni tiwerenge kwa kamphindi chabe za izi, mutu wa 3 ndipo ndime za 3 ndi 4. Tiyeni tiwone ngati izi siziri zolondola.

Kudziwa ichi choyamba, kuti mmasiku otsiriza kudzafika anthu onyoza, oyenda mwa zilakolako za iwo eni,

Ndi kumati, Liri kuti lonjezo la kudza kwake?... kuyambira pomwe makolo anagona muja, zinthu zonse zikupitirira monga momwe izo zinali pachiyambi cha chirengedwe.

Pakuti ichi iwo akukhala osadziwa dala, kuti ndi mwa mawu a Mulungu miyamba inakhala kale lomwe, ndipo dziko linayima mmadzi ndi—ndi mu madzi:

Kotero kuti dziko lomwe...linali, pokhala kuti linamizidwa ndi madzi, linawonongeka:

³³ Tsopano, ife tikuwona kuti chifukwa chimene phunziro ili liri lowalitsidwa, ndi chifukwa chakuti mneneri apa wanena kuti mu masiku otsiriza ano onyozawa adzabwera kumadzanana zinthu izi. Mukuona? Zinaloseredwa. Chifukwa chimene anthu akuchitira lero momwe iwo akuchitiramu... Bwanji, inu zedi mukuyembekezera izo, chifukwa Baibulo linati kuti: “Mu masiku otsiriza adzakhala a m’mutu, odzikuza, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu, okana choonadi, onenera amzawo zabodza, amwano, onyoza iwo amene ali abwino, okhala ndi mawonekedwe a chipembedzo namakana mphamvu yake; kwa oterewo patukani.” Kodi ife tingamayembekezere zina zofanana ndi Choonadi? Zedi!

³⁴ Pamene Mose anapita ku Igupto kukawombola ana a Israeli ndi ndodo yokha m'dzanja lake ngati chitsimikizo, Mulungu Wakumwamba ali naye pambuyo, iye anachita zozizwitsa. Kunadza ochita mowonera pambuyo pa iye nachita chinthu chomwecho chimene iye anachita. Mwaona? Tsopano, iwo anadza kachiwiri iye atachita ichi koyamba. Ndiye iwo anadzanso, chifukwa iwo amangochita mowonera chomwe iye anachita, kuchita mowonera cha pachiyambicho. Ife tikupeza izo. Ndipo tsopano, inu mukuti, “Chabwino, awo anali masiku a Mose.” Koma Malembo omwewo akuti iwo adzabweranso mu masiku otsiriza, “Monga Yanne ndi Yambre anatsutsana ndi Mose, chotero ali anthu awa a malingaliro osokonezeka pa Choonadi.” Mwaona? Zowonera, zinthu za mitundu yonse kuti asokonezere anthu.

³⁵ Ndiyeno, ngati mkwatulo uwu umene ukufika poti uchitike. . . Ndipo chirichonse chimene Mulungu ali nacho mwa mzera wa Mawu Ake, pali nthawizonse chinthu china choti chibwere kudzasokoneza icho ngati iwo angathe. Ndi—ndi—ndi cholinga cha Satana kuti achite izo.

³⁶ Monga m'bale kuno wochokera ku msonkhano uko ku Las Vegas anati, “Satana,” nati “dziko linali ulamuliro wake ndipo—ndipo uko pokhala kulikulu kwake.” Ine ndikudziwa kuti Satana ndi mulungu wa dziko lino. Fuko lirilonse pansu pa Kumwamba limalamuliridwa ndi iye. Ndi momwemo! Dziko ili ndi la Satana. Koma Yesu adzalilanda ilo. Iye analipereka ilo kwa Iye tsiku limodzi, ndipo Iye analikana ilo; koma Iye anati—chifukwa Iye anadziwa kuti Iye adzakhala wolowa wake mu nthawi ziri nkudza.

³⁷ Onyoza, tiyeni tingotenga kwa timphindi tingapo pa liwu limodzilo ife tisanapitirire. Onyoza. . . Ine ndimawerenga pepala pafupi masabata awiri apitawo mu Tucson kuti Mngerezi wina wochokera ku England ananenapo—unali mutu mu pepala—kuti kupachikidwa kwa Ambuye wathu Yesu Khristu kunangokhala zonyengezera pakati pa Pilato ndi Yesu, kuti Iye anadza kudzapanga—kudzangodzipangitsa Yekha chinachake. Ndipo palibe njira yomwe ife tingatsutsire izo kwa iwo, chifukwa zinthu zonse za Mulungu ziyenera kulandiridwa mwa chikhulupiriro. Ife tiyenera kukhulupirira izo. Tsopano, iye anapitirira kufotokoza momwe izo zikanachitikira.

³⁸ Kuno posachedwapa mu dziko lopambanalo, London, mu England kani, kumene John Wesile ndi Charles ndi ambiri a alaliki amphamvu a masiku a oyambirira, Spurgeon ndi iwo uko analalikira Uthenga mu misika ya nsipu ndi kulikonse kumeneko, iwo anawukana Uthenga uwo wa tsiku lawo ndipo onani chomwe iwo ali mu tsiku ili. Ndiko komwe M'bale Williams ndi iwo ali usiku uno. Ndi limodzi la mayiko opanda khalidwe kwambiri mu dziko. Ine ndapita mu dziko lonse, koma ine sindikudziwa chinthu china chomwe chiri

chopanda khalidwe ngati—ngati—ngati England. Ndi... Billy Graham ananena chinthu chomwecho. Bwanji, iye anachita kumuchotsa mkazi wake ku malo awo opumirako, momwe—ujeni—machitidwe a—pakati pa amuna ndi akazi amachitira poyera mu malo opumirakowo. Pamene ine ndinali kumeneko ine sindinawone chomwe chingaswe mtima wa munthu mwa kuchuluka kwina kuposa chomwe chinali kuchitika mu England, komwe anali ndi mwayi ndipo nthawi imodzi anatsogolera dziko lapansi mu kukonzanso. Kungosonyeza momwe zingagwere.

³⁹ Koma inu mukuona chomwe chimachititsa izo, uthenga womwe unapyla pa nthawiyo, Angerezi akuyesa kukangamira uthenga womwewo kwa lero. Izo sizigwira ntchito lero. Izo sizigwira ntchito.

⁴⁰ Zikanatani... Bwanji ngati Mose akanadza nabweretsa uthenga wa Nowa, “Ife timange chombo kuti tiwolokere pa mtsinje wa Nile?” Sizikanagwira ntchito. Ndipo ngakhale Uthenga wa Yesu siukanagwira ntchito ndi Mose. Ndipo ngakhale Uthenga wa Wesile siukanagwira ntchito mwa Lutera kapena uthenga wa Lutera konsekonse. Ndipo lero, ife—kukonzanso kwathu kwakukulu kotsiriza kunali Pentekoste. Ndipo lero ife tikuchoka apo, ndipo Uthenga wa Chipentekoste siwusakanizana ndi uwu, chifukwa ndi tsiku lina. Wonse ndi Mawu a Mulungu, koma ndi chimango. Monga mapazi, mikono, kukwera mmwamba, ndi kupanga Mkwatibwi kuti apite mu mkwatulo. Onani, Iwo siwuli—musawayike anthu awo mmbuyomo posayenera; iwo anakhala moyo mwa uthenga wawo. Onsewo adzabwera amene anali mwa Mkwatibwi. Monga momwe moyo umapyolera mu phesi la tirigu. Iwo umasiya tirigu—thunthulo, koma tirigu amadziwunda yekha, monga njere ya tirigu imene inagwera mu nthaka.

⁴¹ Kuno posachedwapa ine ndinali kuweringa bukhu wachi German wina analilemba motsutsa; iye anati, “Mwa onse a—anthu otentheka mu dziko, William Branham ali pamwamba pa onsewo.” Iye anati, Bwanji, iye sikanthunso koma... Iye ndi—iye ndi wamatsenga. Iye amachita zinthu izi...” Onani, bambo uyu posadziwa... .

⁴² Ndiyeno, bamboyu anali wotsutsa. Iye samakhulupirira ngakhale mwa Mulungu. Iye anati, “Mulungu amene akhoza kukhala mu Mibadwo ya Mdimba, kugwira manja ake pamimba pake, naseka pa gulu la Akhristu pokhala azimayi, ndi omwe amayenera kukhala ophunzira ake omwe—azimayi okhala ndi ana aang’ono ndi zinthu nkulola mikango iwadye iwo ndipo nkusasuntha ngakhale dzanja.” Mukuonatu komwe malingaliro a chithupi, komwe maphunziro ndi zinthu sizingagwire masomphenya? Mbewu ija ya tirigu inayenera kugwera mu nthaka.

⁴³ Monga ngati Yesu anayenera kugwa kuti awukenso, choteronso mpingo wa Pentekoste unayenera kugwa. Unayenera kugwera mu nthaka, Mibadwo ija ya Mdimu. Tirigu aliyense amene—njere iliyonse imene ipita mu nthaka, iyenera kukhala mu nthawi ya mdimayo kuti idzabale. Koma iyo inayamba kumera mwa Marteni Lutera. Nibwera kupyolera mwa Wesile, mpaka kudzafika mu Pentekoste; tsopano kupita mu—kupita ku njere. Ndipo tsopano, kachitidwe ka chipembedzo kamene iwo anasiya mmbuyo, iwo ndi mapesi. Ndizo zonse. Ziyenera kuwotchedwa, m'chitidwe wa chipembedzo. Koma njere yeniyeni ya tirigu imene inatuluka mu kukonzanso kulikonse kuja idzakwatulidwa mwa Mkwatibwi. Zonsezo palimodzi zidzapanga Mkwatibwi.

⁴⁴ Tsopano, ife tikupeza kuti mu England uko iwo anachita mosanzira kupachikidwa kwa Ambuye osati pakale, gulu la anthu amenewo, ilo lalitali—ana okhala ndi tsitsi lalitali aja ndi zinthu namafuwula—kumutcha Yesu “adadi-o” ndi zonyansa zonsezo. Uve woterowo . . .

⁴⁵ Tsopano, inu mukuti, “Uko ndi ku London, England.” Taonani zomwe zinali mu pepala sabata yatha kuno ku Amerika. Dokotala wina wotchuka wa zauzimu wochokera ku sukulu yapamwamba anati kuti—kupachikidwa kunali kunyengezera, nati kuti Yesu ankangofuna kudzipangitsa Iyeyekha chotero, kuti Iye anamwa maudzu a mandrake awa, ndikuti. . . Ife tikupeza zimenezo mu Genesis pamene zinanenedwa. Ndi maudzu onga ngati chamba kapena chinachake. Zimapezeka ku Orients uko. Ndipo ngati inu muwamwa, akugonetsani inu, mwina mwanu—ngati mwafa, kukomoka, chirichonse kwa masiku awiri kapena atatu panthawi.

⁴⁶ Iye anati pamene iwo anamumwetsa Iye vinyo wosasa ndi ndulu, nkotheka kuti zimenezo zinali mawudzu a mandrake. Ndipo pamene iwo anatero, iwo anamuptsa Iye izo; ndipo Iye anapita ndipo analefuka ngati anali atafa. Iwo anakamuyika Iye mmanda, ndipo iwo anamugoneka Iye mmenemo. Ndipo patapita masiku awiri kapena atatu, ndithu, kubweranso ndiye Iye anawukanso, anali wabwino basi. Akuti Iye anapita ku India nakafa kwinakwake imfa wamba. Kuyesa kunamizitsa chipembedzo. Malo oyamba, wotsutsa ameneyo. . . Kodi vuto la anthu ndi chiyani? Mwaona? Ndi chabe tsiku ili lomwe tikukhalamoli, onyoza (mwaona?) tsiku kuti akwaniritse uneneri.

⁴⁷ Mulungu anagawa Mawu Ake kwa m'badwo uliwonse. Ndipo uliwonse wa mibadwo imeneyo umangowonetsera izo. Ndiponso anakonzeratu anthu ku m'badwo umenewo kuti akwaniritse Mawu amenewo. Nthawi iliyonse imene Iye anagawa Mawu Ake, Iye anagawa munthu wake. Pamene Iye anagawa nthawi ya Mose, Iye anagawa Mose kwa iyo. Pamene Iye anagawa nthawi ya Mwana wa Mulungu kuti abadwe,

Iye anagawa Iye kwa iyo. M'badwo uliwonse Iye anagawa anthu Ake, kuwakonzeratu. Monga Baibulo linanenera, palibe chinthu... Ngati Mulungu ali wopanda malire, wamphamvuzonse, yense wodzaza mphamvu, okhala paliponse, odziwa zonse, bwanji, Iye anadziwa zinthu zonse kuchokera kuchiyambi. Kotero Iye anadziwa... Palibe chirichonse pamalo osayenera; ndi ife tokha amene timaganizira kuti ziri...?... chirichonse chimayenda...

48 Yang'anani mmbuyo mu Mawu Ake ndi kuwona zomwe Iye akuchita, ndiye ife tidzakhala ndi kumvetsa.

49 Tsopano, ingoganizani. Malo oyamba, ngati mlaliki ameneyo akanaganiza, pamene iwo anathira vinyo wosasa ndi ndulu mkamwa Mwake, Iye anazilavula izo. Iye sanadzimwe izo poyamba pomwe. Mwaona? Ndi onyoza chabe amene akutulukira. Chinthu china, anachita bwanji Yesu uyu wa ku Nazareti, moyo Wake unagwirizana bwanji ndi uneneri uliwonse wa Chipangano Chakale? Zikanakhala motani. Sizikanakhala popanda izo kukhala zokonzedweratu ndi Mulungu. Moyo Wake unagwirizana ndi uneneri uliwonse wa Chipangano Chakale. Chinthu china, ngati ophunzira aja ananamizira za Iye chotero, chifukwa chiyani aliyense wa iwo anafa mwakufera? Ndipo ngakhale mtumwi Petro anati, "Muzondotse mutu wanga pansu; sindine woyenera kufa monga Iye." Motani... Iwo anamutenga Andreyana namukhomera pa mtanda cha m'mbali. Iwo aliyense anasindikiza umboni wawo mu magazi awo omwe. Iwo anamkhulupirira Iye, namkonda Iye, ndipo anapereka miyoyo yawo chifukwa cha Iye. Ngati Iye anali wonyengezera, iwo akanachita bwanji izo? Onani, kuchita mwauzimu, anthu samamvetsa iko.

50 Kuno kunali munthu wotchuka sikale kwambiri, Rabbi wina wotchuka, amene analemba kuti Mose pamene ankapyola mu Nyanja Yofiira, anati, "Sanali madzi enieni; madzi sanapange makoma." Nati, "Chomwe chinali, uko kumapeto ake a Nyanja Yakufa, kunali bango lambiri, ndipo iye anapyola mu madziwo—mabango, bango la mmadzi. Munalibe madzi mmenemo, bango lokhalokha, nyanja ya—ya bango ndi yomwe iwo anadutsapo." Ndipo alaliki ambiri amakhulupirira izo; iwo—ndipo amavomereza izo.

51 Kuno osati kale kwambiri pamene wokayenda pamwezi woyamba anakwera mmwamba, iye anabwerera ndipo iye sanawone kalikonse ka Mulungu. Ngakhale icho chinawatembenuza atumiki. Iwo ankaganiza Mulungu amakhala kumeneko kwina kwake mailosi zana ndi makumi asanu mmwamba. Bwanji, mai, motani... Maphunziro ndi nzeru za dziko lino zatembenuza mpingo kukhala mulu wa zinyalala zasanza. Apo... Ziri...

⁵² Maphunziro, ndi dongosolo la maphunziro, sayansi, ndi chitukuko ndi za mdierekezi. Ndi chitukuko cha mdierekezi. Baibulo linatero. Ndipo chitukuko chatu chimene chikubwera sichidzakhala ndi chochita nacho chitukuko ichi konse. Si kalikonse ka izi konse. Icho chidzakhala chitukuko chosiyana. Mu chitukuko ichi ndi dziko ili la sayansi lomwe ife tiri naloli. . . Sayansi yochuluka—mwasayansi tikukhala, mopitirira tikupita mu imfa, zinthu, misampha yoti itiphe, ndi chirichonse. Mu chitukuko chatsopanocho simudzakhala imfa, mopanda matenda, zosautsa, kapena mopanda zowawa. Mwaona? Sikudzakhala chirichonsecho mmenemo. Kotero chitukuko ichi chiyenera kudzawonongedwa, chifukwa ndi cha mdierekezi.

⁵³ Ife tikupeza kuti mu Genesis 4 kuti anthu a Kaini anayambitsa chitukuko, kumanga matauni, ndi mizinda, ndi zina zoterozo, ndi zipangizo za nyimbo, nakhala mu sayansi. Ndipo anthu anatalikira kwambiri kwa Mulungu, komabe achipembedzo. Koma pamene anthu a Seti anadzapo, iwo anayamba kudza pa—kuyitana pa Dzina la Ambuye. A, kunena za. . .? . . .

⁵⁴ Ine sindiri pano kuti ndipweteke malingaliro a aliynse, kapena kunena chinachake chokhudza mpingo. Ndipo ngati inu muli pano ndipo ndinu a mu mpingo uwu, ine sindikunena izi kuti ndipweteke mmalingaliro anu, chifukwa muli anthu abwino ambiri mmenemo monga momwe aliri mu mipingo yina. Koma ine ndimawerenga mu Shreveport sabata yatha pamene mpingo wa Katolika unalankhula mawu. Ndipo ife tikuwona pamene iwo onse akudza palimodzi tsopano pa bungwe lotchuka la mipingo ndi zina zotero mongokwaniritsa kwenikweni zomwe Baibulo linati iwo adzachita. Mofanana kwenikweni. . .

⁵⁵ Tsopano, ife tikupeza kuti iwo anati, “Bwanji, Baibulo,—ena mwa Aprotestanti akufuna kugwirisitsa kwa Baibulo ilo. Bwanji,” anati, “Baibulo silinali kanthu koma Bukhu, mbiriyakale ya mpingo, ndipo iwo analibe Ilo mu Zowerenga mpaka pafupi zaka mazana awiri ndi makumi asanu zapitazo. Nthawizonse wakhala uli mpingo.” Nati, “Unali mpingo osati Baibulo, ndipo Baibulo ndi mbiriyakale chabe ya chomwe mpingo unachita.” Ndi bodza lothyathyalika bwanji limenelo. Bwanji, ife takhala nalo Baibulo kwa zaka mazana atatu. Chipangano Chakale chinalembedwa mwa Malembo kwa zaka mazana mazana Khristu asanadze. Ilo linali bodza lothyathyalika chabe la mdierekezi.

⁵⁶ Ndipo ife tikupeza mu tsiku ili pamene kunyoza kopambanaku ndi kulipangitsa Baibulo kukhala choseketsa ndi kuyesa kulikankhira Ilo kunja. . . Mulungu ayenera kuweruza mpingo ndi chinachake. Iye sangakhale wolungama. . . Iwo sangangobwera mu msewu uwu ndi kudzandimanga ine ndi kuti ine ndikuthamanga mailosi makumi atatu pa ora mu chigawo cha mailosi makumi awiri pokha patakhalala chinachake

pamenepo choti chindidziwitse ine kuti ine ndikuloledwa kuthamanga mailosi makumi awiri okha. Ziyenera kukhala pamenepo. Ndipo Mulungu adzaweruzwa mpingo—adzaweruzwa anthu tsiku lina. Ife tikudziwa izo. Pali chiweruzo chikubwera. Kotero ngati Iye akuti adzaweruze ilo ndi mpingo wa Katolika, mpingo wa Katolika wake uti? Ngati Iye ati adzaweruze iwo mwa Methodist, Abaptisti atayika. Ngati Iye adzaweruzwa iwo ndi a umodzi, a uwiri atayika. Mwaona? Nanga Iye adzaweruzwa iwo ndi chiyani? Iye anati Iye adzaweruzwa iwo ndi Khristu, ndipo Khristu ndi Mawu. Kotero ndi Mawu a Mulungu amene Mulungu ati adzaweruzire. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi nadzakhala pakati pathu... Yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse.” Mwaona? Kotero Iye adzaweruzwa iwo mwa Mawu Ake.

⁵⁷ Ndipo tsopano, ife tikupeza kuti mu tsiku ili pamene iwo akuyesa kulikankhira Baibulo kunja, kuvomereza mpingo... Baibulo, osalifuna ilo—mpingo—kotero iwo akhoza kungopanga chiphunzitso cha mtundu uliwonse kapena china chirichonse namayenda mwa icho.

⁵⁸ Bwanji, monga ine ndinkanenera usiku wina ku Shreveport mwa izo—mgonero pamene iwo ankapha mwanawankhosa wa nsembe, panayenera kukhala popanda chotupitsa pakati pawo pa masiku asanu ndi awiri onsewo. Popanda chotupitsa, mkate wosatupitsidwa. Chirichonse chinayenera kukhala chosatupitsidwa. Izo zinali zoyimirira Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo yomwe timayipeza mu bukhu umu. Ndipo palibe chotupitsa pamene ziri—zina zitasakanizidwa nawo. Ndipo ife tiri ndi ziphunzitso zosakanizika, ndi chipembedzo, ndi china chirichonse palimodzi ndi Mawu ndi kumayesabe kuzitcha Izo Mawu. Pasakhale chotupitsa masiku asanu ndi awiri onsewo. Ndipo ngakhale zomwe ziti zidyedwe lero, musayese kuzisunga izo mpaka mawa, mudziwotche izo ndi moto dzuwa lisanatuluke dzuwa, pakuti pali uthenga watsopano umene ukudza ndi chinthu chatsopano.

⁵⁹ Onani, kuyesa kusunga mpakana. Koma ilo lakhala khalidwe la mpingo. Chitsitsimutso chimadutsa, chinthu choyamba inu mukudziwa, pafupi zaka zitatu iwo amayamba bungwe pa icho. Chipembedzo chimayamba bungwe. Koma kodi inu mwazindikira, ichi chakhala chikusesa kwa zaka makumi awiri tsopano, ndipo palibe bungwe. Ndipo silidzakhhalapo konse! Awa ndi mapeto. Tirigu wabwereranso ku tirigu. Tirigu wabwereranso ku njere yake. Mankhusu akanuka kwa iye. Ndipo tirigu ayenera kugona pamaso pa dzuwa kuti akhwimitsidwe.

⁶⁰ Kodi sichinthu chachirendo kuti posachedwapa ku Gombe la Kum'mawa, mdima waukulu. Iwo sanakhoze kuwumvetsa iwo. Texas anachita mdima sabata yatha. Iwo sangathe kumvetsa

izo. Kodi inu simukuzindikira kuti icho ndi chizindikiro? Kodi inu simukudziwa kuti mafuko akusweka? Israeli ali ku dziko la kwawo, ndipo zizindikiro izi zikusonyeza kuti ife tiri kumapeto! Nthawi yomweyo kukuchita mdima, kodi inu simukudziwa izo ndi zizindikiro zimene mneneri anazinena kuti—“Koma kudzakhala Kuwala nthawi ya madzulo,” kuti kudzakhala Kuwala komwe kuti kudzatulukire nthawi ya madzulo pamene midima ndi zinthu zikuchitika mwa njira yomwe ziririmu tsopano. Yang’anani momwe mdima unadzeramu.

⁶¹ Papa atangobwera kumene kuno. Kumbukirani ku kachisi pamene iwo—inu muli nawo matepi—ndikulingalira kuti inu nonse mumawatenga iwo—momwe Ambuye anawonetsera kujaku tsiku lija mu kachisi chimodzimidzi kumene mibadwo ya Mpingoyo ikanadzakhala ndi momwe ikanati idzakhali. Ndipo ine ndinayijambula iyo pa bolodi pajapa, mibadwo ya mpingo ija yomwe inu mukuyiwona apa itajambulidwa mu bukhu. Ndipo ngati Mzimu Woyera uwo ukanati usatsike mu Lawi la Moto lalikulu nupita kumbuyo pakhomapo nuyijambula iyo mwa Iwowokha pamene atatu kapena anthu mazana anai anakhala akuyang’ana pa izo. Ndipo pamene papa anangowuyamba wa kuno, mwezi mwa njira yina unadetsedwa, ndipo iwo anajambula zithunzi, mofanana ndi momwe zinajambulidwira pa nsanja paja. Tsopano, iye anapanga ulendo wa kuno pa 13, anayenda masitepe 13, nadya mgonero ndi anthu 13, kwa fuko limene liri nambala 13, ndipo mdima kubwera kulikonse. Kodi inu simukuwona komwe ife tiri? Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

⁶² “Onyoza adzawuka mmasiku otsiriza, kumati, ‘Palibe kusintha kwa nthawi kosiyana ndi momwe zinaliri, mosiyana ndi pamene makolo athu anagona.’” Koma pamene inu muwona zinthu izi zikuyamba kuchitika, dzutsani mutu wanu; konzekani; chinachake chikhoza kuchitika pa nthawi iliyonse. Khristu kudzera Mpingo Wake.

⁶³ Tsopano, iwo sakuzikhulupirira izi, chifukwa ziri... Ziri... Iwo—Iwo ali... Iwo sakuzindikira kuti ndi iwo amene akukwaniritsa Malemba. Anthu ndithudi samazindikira pochita zinthu izi ndi kulankhula zinthu izi kuti iwo akukwaniritsa Malemba. Ankadziwa pang’ono bwanji Kayafa wansembe wamkulu ndi ansembe onsewo mu tsiku limenelo amene ananyoza namuseka Iye—sankamudziwa kuti ndi Mulungu yemwe ankamuyimba, “Mulungu Wanga, Inu mwandisiyiranji Ine (Salimo la 22), manja Anga ndi mapazi Anga, iwo awalasa...” Kumayimba izo m’kachisi ndipo Iye kumafa kunja kuja pamtanda, iwo amangodziwa moperewera kuti iwo anali akuchita zimenezo. Ngakhale Yesu anapemphera, “Atate, akhululukireni iwowa. Iwo sakudziwa chimene akuchita.” Chifukwa iwo anachita kuloseredwa kwenikweni mwa Malemba kuti adzakhala akhungu.

64 Kodi inu mumadziwa kuti mpingo wa Protestanti ndi wa Katolika unaloseredwa mu masiku otsirizawa kuti adzakhala akhungu, chinthu chomwecho mu Malemba, ndi Khristu ali kunja kuyesa kuti alowe mkati? “Chifukwa iwe ukuti ine ndi wolemera ndipo sindisowa kanthu, sukudziwa iwe kuti ndiwe womvetsa chisoni, wosawuka, wopanda pake, wamaliseche, ndi wakhungu, ndipo sukudziwa izo!” Chivumbulutso 3. Ndi zimenezotu, kubwereranso ku khungu, kupondereza pa zinthu za Mulungu kukhala ngati izo—izo sizinatanthawuze kanthu kwa iwo, kunyoza ndi kuseka izo; ndi zimene Baibulo linanena.

65 Koma kwa Mpingo, Mkwatibwi, mkwatulo ndi vumbulutso kwa iye. Izo zawululidwa kwa iye, kuti vumbulutso, Mkwatibwi woona wa Khristu adzakhala akuyembekezera vumbulutso ilo la mkwatulo.

66 Tsopano, ndi vumbulutso, pakuti vumbulutso ndi chikhulupiriro. Inu simungakhale ndi vumbulutso ilo nkusakhala chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndi vumbulutso, chifukwa ndi chinachake chimene chawululidwa kwa inu. Chikhulupiriro ndi vumbulutso. Chikhulupiriro ndi chinachake chimene chawululidwira kwa iwe monga momwe zinaliri kwa Abrahamu, chomwe chinakhoza kutcha chirichonse chosiyana ndi chomwe chawululidwa kwa iye monga ngati kulibe. Tsopano chikhulupiriro...Ndicho chomwe chikhulupiriro chiri, ndi vumbulutso la Mulungu. Mpingo wamangidwa pa vumbulutso, thupi lonse lathunthu.

67 Kuno masabata angapo apitawo ine ndimalankhula kwa mlaliki wabwino wa Baptisti. Iye anadza kudzakambirana nane. Iye anati “Ine ndimakukondani inu ngati munthu, koma,” anati, “ndinu wosokonezeka kwathunthu.”

Ine ndinati, “Ndiye ine ndikukupemphani inu mundithandize ine ndiwongoledwe...” Tsopano, iye anati... “ndi Lemba.”

Iye anati, “Ife sitidzakhoza konse, M’bale Branham, kuzibweretsa zinthu palimodzi mpaka ife titatenga liwu lililonse pa liwu pa liwu chimodzimodzi ndi Chigriki ndi zina zotero.”

68 Ine ndinati, “O, bwana, inu mukudziwa bwino koposa izo.” Ine ndinati, “Ngakhale mu Nicene Council, kale chotero, zaka mazana atatu imfa ya Khristu itachitika, iwo anali akutsutsana zoti ndi sikolala uti wa Chigriki amene anali wolondola. Inu simungathe... Ndi vumbulutso. Chinthu chonsechi chiri...”

Iye anati, “Ine sindingalilandire vumbulutso.”

Ine ndinati, “Ndiye inu mungamulandire bwanji Khristu?”

Iye anati, “Bwanji, Baibulo linati, ‘Iye amene akhulupirira ali—ali—pa Yesu Khristu ali ndi Moyo Wosatha.’”

69 Ine ndinati, “Izo nzowona. Ilo limatinso kuti palibe munthu amene angamutche Yesu Khristu koma mwa vumbulutso la

Mzimu Woyera limene linawululidwa kwa iye.” Mwaona? Ndi pamenepotu, zabwereranso mmbuyo, kugweranso mmbuyo ku Vumbulutso. Ziyenera kuwululidwa.

⁷⁰ Mu Baibulo...Kaini ndi Abele analibe Baibulo loti awerenge, koma zinawululidwa kwa Abele mwa chikhulupiriro, chomwe chiri vumbulutso. Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yabwino koposa ija ya Kaini, imene Mulungu anamuchitira umboni nayo kuti iye anali wolungama. Pamene Yesu anafunsidwa apa mu Mateyu 16:17 ndi 18...Ife tiribe nthawi yowerenga izo, koma ngati inu mukufuna kuwalemba. Iye anati, “Kodi anthu amati Ine, Mwana wa munthu ndine, yani?”

Wina wa iwo anati, “Inu ndi Mose, Eliya, kapena winawake.”

Iye anati, “Koma Inu mukuti Ine ndine yani?”

⁷¹ Iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu Wamoyo.”

⁷² Iye anati, “Wodala ndiwe, Simoni, mwana wa Yona, pakuti thupi ndi magazi sizinakuwululire iwe izi; Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe. Pa thanthwe ili (vumbulutso lauzimu loti Mulungu ndi Ndani, Yesu ndi Ndani, ndipo Iye ndi vumbulutso la Mulungu, Mulungu atapangidwa mwathupi nawululidwa kwa dziko. Iye anali mu dzikoli; Mulungu anali mwa Khristu kuliyanjantsa dziko kwa Iyemwini, kuwulula chomwe Mulungu anali mu thupi la mnofu)...” “Inu ndi Khristu, Wodzozedwayo, Mwana wa Mulungu.”

⁷³ Iye anati, “Thupi ndi magazi sizinawulule izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe. Pa thanthwe ili, Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga (vumbulutso la Mawu mu nyengo Yake)—Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga ndipo zipata za gehena zisingawugonjetse iwo.”

⁷⁴ Bukhu la Chivumbulutso ndi Bukhu lotsiriza la Baibulo. Ilo ndi lotsekeka kwa osakhulupirira. Mmenemo Baibulo limati mu mutu wa 22, “Aliyense amene adzachotsapo liwu limodzi kwa Ilo kapena kuwonjezera liwu limodzi kwa Ilo, Ine ndidzachotsa gawo lake mu Bukhu la Moyo.” Ife tikuzindikira kuti ndiye Izo zonse zinaperekedwa kwa okhulupirira. Ndipo izo zimatsegula Bukhu la Chivumbulutso ndi kuwulula Amene ali Mlembi wa Bukhu lonse ili (Iye ndi woti ukamuyang’ana ali Alfa ndi Omega, kuyambira ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, Yesu Khristu chimodzimidzi basi monsemo), nawulula chinsinsi Chake chonse cha Iyemwini ndi madongosolo Ake kwa mibadwo Yake ya Mpingo yomwe ikudza, ndipo inasindikizidwa mmenemo ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri.

⁷⁵ Tsopano, Bukhu linalembedwa, koma ndiye kumbukirani, Ilo linasindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri’zi sizinali zoti zitsegulidwe, Chivumbulutso 10, mpaka pa kuwomba kwa mngelo wa padziko

pansi pano, Chivumbulutso 10:7. Mwaona? “Ndipo mu masiku a kuwomba kwa Uthenga wa mngelo wotsiriza, mngelo wa chisanu ndi chiwiri, chinsinsi cha Mulungu chiyenera kutsirizidwa mu m’badwo umenewo.” Uwo . . . Ndipo ndiwo m’badwo umene ife tikukhalamowu.

⁷⁶ Ife tonse tikudziwa kuti tikukhala mu m’badwo wa Laodikaya. Sikudzakhalanso m’badwo wina kwa iwo; sizingatero. Kotero ife tikukhala mu M’badwo wa Laodikaya, ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi zimene zamata Bukhu ilo ndi chinsinsi kwa anthu, ziyenera kutsegulidwa mu tsiku limenelo. Ndi zimene Iye analonjeza. Tsopano, sizikhala chinachake cha kuna kwa Mawu, chifukwa inu simungawonjezere ku Mawu kapena kuchotsa pa Mawu. Iwo ayenera kukhala nthawizonse Mawu. Koma vumbulutso ndi loti liwulule Choonadi cha Iwo, chomwe Iwo ali, kuwapangitsa Iwo kuti agwirizane ndi Malembo ena onse. Ndipo kenako Mulungu awatsimikizira iwo kukhala Choonadi.

⁷⁷ Onani, Mulungu samasowa womasulira. Iye ndi Wodzimasulira Yekha. Iye amachita kumasulira Kwayekha pokwaniritsa zinthu zimene Iye anati zidzachitika. Monga pachiyambi Iye anati, “Kuwale!” ndipo kunawala. Izo sizisowa kumasulira kwina kulikonse. Izo zinatsimikiziridwa.

⁷⁸ Tsopano, Iye analonjeza zinthu zina mu tsiku lotsiriza lino mu Lemba. Bwanji, ndi zimenezotu. Ndi momwe Yesu analiri Mwana wa Mulungu. Iye analonjeza kudzamutumiza Iyeyu. Pamene Iye anali mmasiku Ake pansi pano ndipo anthu samakhoza kumukhulupirira Iye, Iye anati, “Fufuzani Lemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli ndi Moyo Wamuyaya; ndipo Iwo ndi Iwo amene amachitira umboni za Ine. Ngati Ine sindichita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine ayi. Koma ngati inu simungandikhulupirire Ine, khulupirirani ntchito zomwe Ine ndizichita; chifukwa izo zimachitira umboni woti Ndine yani.”

⁷⁹ Chabwino ndiye, mu m’badwo wa Wesile ntchito zomwe iye anachita zinachitira umboni wa yemwe iye anali. Mu m’badwo wa Lutera pa kukonzanso, bwanji, ndithudi zinachitira umboni wa yemwe iye anali. Mu masiku a Achipentekoste, kubwezeretsanso kwa mphatso, kubwezeretsa kwa mphatso, kulankhula mmalirime, ndi kutulutsa ziwanda, ndi mphatso, bwanji izo zinkachitira umboni. Panalibe nthabwala pa izo.

⁸⁰ Anthu anati pamene izo zinatulukira poyambirira . . . Ine ndinawerenga mabuku pa mbiriyakale ya Pentekoste. Iwo anati, “Sizingapitirire nthawi yaitali; zizirala.” Zikuyakabe. Bwanji? Ndi chifukwa inu simungazizimitse izo. Mulungu anati zikhalapo. Ndi gawo limenelo la Mawu, ndipo inu simungathe kuwazimitsa iwo koposa . . . Ndiyeno pamene Mkwatibwi akutulutsidwa, inu muzizimitsa bwanji izo? Ndi

vumbulutso la kukwaniritsika kwa Mawu kukhalitsidwa owona. Ndipo ife tikukhala mu tsiku limenelo. Mulungu alemekezeke! Vumbulutso la chinsinsi la Iyemwini.

⁸¹ Tsopano, mkwatulo uli kokha, mkwatulo uwu umene ife tikuwunenawu ndi wa kwa Mkwatibwi yekha. Kumbukirani, Baibulo linati, “Ndipo ena onse akufa sanakhale ndi moyo kwa zaka chikwi.” Mkwatulo wopambanawu... Ngati kulibe mkwatulo amzanga, ife ndiye tiri pati? Ife tichita chiyani? Ife tikukhala mu m’badwo uti? Ife tiri ndi lonjezo lanji? Padzakhala mkwatulo. Baibulo likutero kuti udzakhhalapo; ndipo udzangokhala kwa Osankhidwa okha, Mkazi wosankhidwa, Mkwatibwi mu tsiku ili amene wakokedwera kunja, Mpingo.

⁸² Liwu lomwe loti *mpingo* limatanthawuza, “oyitanidwa kuchokera.” Ndipo monga Mose anayitana fuko kuchokera mu fuko, Mzimu Woyera ukuyitana Mkwatibwi kuchokera ku mpingo. Mpingo kuchokera mu mpingo, ziwalo kuchokera ku chipembedzo chirichonse kupanga Mkwatibwi, Mtengo wa Mkwatibwi, ziri mu—mu tepi, Mtengo wa Mkwatibwi. Mkwatibwi kutuluka atayitanidwa... Ndipo ndi ameneyo yemwe ali Mtengo wa Mkwatibwi—Mkwatibwi, kani, ndi amene ati adzakhalepo mu mkwatulo, ameneyo yekha, popanda china koma Mkwatibwi, osankhidwawo odziwidwiratu ndi Mulungu kuchokera pachiyambi, mbewu yauzimu ya Atate.

Ndiroleni ndiyime kaye apa miniti chabe, iyo... Ine ndikuchita manjenje kuganiza kuti ine ndikukukhazikani—ndikukhazikani inu motalika kwambiri.

⁸³ Koma tawonani; yang’anani! Aliyense wa anthu inu, kodi mukudziwa zaka inu musanabadwe inu munali mwa abambo anu ngati mbewu? Izo nzolondola! Nyongolosi ya mbewu inali mwa abambo anu, imachokera kwa chiwalo chachimuna, osati chachikazi. Mwaona? Chachikazi chimapereka dzira, malo omererapo, koma nyongolosi imachokera kwa... .

⁸⁴ Tsopano, titi mwa bambo anga kapena mwana wanga wakhala apayu. Pamene ine ndinali wa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi zakubadwa, mwana wanga anali mwa ine. Ine sindimamudziwa iye, koma iye anali mnenemo. Tsopano, kupyolera pa nthaka yomererapo, kupyolera mu chikwati choyera, iye akukhala mchifanizo cha ine. Ine ndikumudziwa iye; ine ndikhoza kuyanana naye. Ndipo iye angobwera pa nthawi pamene ili nthawi yoyenera.

⁸⁵ Tsopano, kotero inu munali mu... Ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, inu munali—mwa Mulungu pasanakhale dziko. Inu muli gawo, mwana wa Mulungu, lingaliro la Mulungu. Iye anadziwa m’badwo womwe inu munali kudza. Iye anakukonzeranitu inu ku m’badwo umenewo kuti mudzatenge malo amenewo, ndipo palibe wina amene angawatenge iwo... . kaya ndi zowonera zingati ndi zinthu, inu muyenera kukhala

pamenepo, chifukwa Iye anadziwa kuti inu mudzakhala pamenepo. Tsopano, inu mwawonetseredwa; tsopano inu mukhoza kuyanjana ndi Iye, ndipo ndi chimene Iye akufuna. Iye akufunitsitsa chiyanjano, kuti azipembedzedwa. Koma mwa—ngati moyo wanu siwunali uli nthawizonse monga lingaliro mwa Mulungu, ndinu wotsanzira chabe wa Chikristu. Mwaona? Akhalapo mamiliyoni ndi mabilyoni a iwo amene angokhala otsanzira chabe Chikristu.

⁸⁶ Ndemanga yomwe ine ndinapanga posachedwapa. Ine ndimayang'ana M'bale Demos Shakarian kumeneko pamene iwo anali—amapanga ng'ombe za haibridi, ndinayang'ana ma chubu oyesera ndi zina zotero zikutengedwa ndi adokotala ndikuyang'ana zinthu izi.

⁸⁷ Mu zenizeni zotuluka kuchokera mu yamphongo mumakhala mwina nyongolosi miliyoni zomwe zimatuluka kuchokera mwa yamphongo mu nthawi imodzi. Ndipo mwinamwake mazira miliyoni amatuluka kuchokera mwa yaikazi pa—nthawi yomweyo. Koma kodi inu mumadziwa mu nyongolosi zonse zazing'onozo zikuyendayenda, miliyoni za izo, pamakhala imodzi chabe ya izo imene imakonzedwera ku moyo, ndipo pamakhala dzira limodzi lokha lachonde? Ndipo nyongolosi yaying'onoyo imakwawa kupyola iliyonse ya nyongolosi zina zazing'onozo, pamwamba pomwe pa nyongolosi iliyonse yowoneka chimodzimodzi ngati iye, ndi kufika pa izo ndi kubwera kuno ndi kudzapeza dzira lachondelo ndi kukwawira mwa ilo. Ndiyeno zina zonsezo zimafa. Bwanji, kunena za kubadwa mwa namwali, bwanji, sichiri chachinsinsi mwatheka ngati—ngati kubadwa kwa mwathupi, momwe zimadziwidwiratu, kukonzedweratu ndi Mulungu.

⁸⁸ Tsopano, pachiyambi, kale mmbuyo, kutali zaka zapitazo isanati nthawi iyambe, inu, ngati ndinu Mkhristu wobadwa kachiwiri usiku uno, inu munali mwa Mulungu pamenepo, Atate anu. Ndicho chifukwa chake pamene inu munabwera mmoyo uno kuno ndi kudzitcha wa Chikristu, chirichonse chikuyenda molakwika, inu mumadabwa bwanji izi ndi zina zonsezi. Ngati... Inu mumadabwa pa izo. Koma tsiku lina chinachake chinakukhudzani inu. Chinali chiyani icho? Moyo uja umene unali mkatimo kuchokera pachiyambi. Ndipo Ngati...?...

⁸⁹ Kanthano kanga ka mphungu kupeza—mayi wake kuipeza mphungu. Inu mwandimva ine ndikulalikira pa izo, momwe mphungu yaing'onoyo inaswedwera pansu pa nsoti. Koma iye... Zizolowezi zake zomayesa kutidyetsa ito—ito tianapiye, kamphungu kakang'ono kaja sikankamva nazo bwino mmimba, chifukwa iye sanali mwanapiye poyamba pomwe, komabe iko kanali mu khola palimodzi ndi anapiye ndipo kankatsatira tianapiye. Koma iko kankakhoza kumapalasa nawo mkhola ndi zinthu, ndipo kamphungu kakang'onoka sikamadziwona bwino izo. Koma nthawi iliyonse iwo ungangoyitana ndi zonse,

tianapiye tonse tating'ono timapitako, kotero iko kankapita nawo.

⁹⁰ Koma tsiku lina mayi wake anadziwa kuti iye anayikira mazira awiri, osati limodzi. Panayenera kukhala lina kwinakwake. Iye anapita kukalisaka ilo. Akuwuluka ponseponse, mozungulira, potsiriza anafika pa khola lina, ndipo iye anamupeza mwana wake. Ndipo iye anafuulira kwa iye. Linali liwu limene iye analizindikira kuti icho ndi chinthu chomwe chikukwanira. Icho ndi chomwe iye ankayang'anira. Mwaona? Ndipo iye anazindikirano kuti iye sanali nkhuku; iye anali mphungu. Ndipo umu ndi momwe ziriri ndi Mkristu wobadwa kachiwiri aliyense. Pamene inu mubwera, ine sindikusamala kuti inu mwakhala mutajowina zipembedzo zingati, mayina angati inu munalembetsa dzina lanu mmabukhu ndi zina, pamene Mawu a Mulungu enieni atsimikiziridwa nakhala owona pamaso panu, chotero, inu mumazindikira ndinu mphungu pomwepo. Chifukwa kuluku wa nkhuku yenseyu, inu kujowina ichi, ndi kujowina *ichi* ndi kupita njira *iyi* ndi njira *iyi*, ndi zopanda pake. Ndi kuwonjezera kwenikweni Mawu kwa Mawu.

⁹¹ Pamene nyongolosi ifika mu chiberekero cha—chachikazi, iyo siimatengera... Inu—inu simumakhala nyongolosi ya munthu mwa abambo anu, ndiyeno chinthu chotsatira inu kukhala nyongolosi yochokera kwa galu, ndipo chinthu chotsatira kuchokera kwa mphaka, ndipo chinthu chotsatira kuchokera kwa nkhuku; inali zonse nyongolosi ya munthu. Ndipo Thupi la Yesu Khristu, Mkwatibwi, likhala gawo la Thupi Lake limene liti lidza... Iye anali Mawu, ndipo Mkwatibwi ayenera kukhala Mawu, Mawu kuwonjezera pa Mawu owonjezedwa pa Mawu. Kulungamitsidwa kwa Lutera, Kuyeretsedwa kwa Wesile, Ubatizo wa Pentekoste kwa Mzimu Woyera, kubwezeretsa kwa mphatso, ndi zina zonsezo zimachitikira palimodzi. Ayenera kukhala Mawu pamwamba pa Mawu, nyongolosi pamwamba pa nyongolosi, moyo pamwamba pa moyo, kuti zikawonetsere thunthu lonse la Mkwatibwi wa Ambuye Yesu Khristu.

⁹² Tsopano inu kumbukirani, inu munali lingaliro. Ndipo tsopano chinthu chake ndi ichi, pambuyo pake ife tikupeza kuti zinthu izi, kuti Khristu akudzera Mkwatibwi Wake, tsopano nanga ife timalowa bwanji mwa Mkwatibwi ameneyo? Tsopano, ndilo funso. Ambiri amati, “Zajowineni gulu lathu.” Ena a iwo amafuna ubatizo wa mtundu winawake. Ena akufuna achite *izi* kapena *izo*. Ena amati ulankhule ndi malirime ngati ayi iwe ulibe icho; ena amati iwe siwusowa kulankhula mmalirime. Awa amati iwe uyenera kuvina mu Mzimu. Ndipo *awa* akuti iwe uyenera kufuula. *Awa* ali ndi zotengeka. Izo zonse nzolondola, ndiyeno komabe izo zonse nzolakwika. Angathe bwanji munthu amene—kapena mkazi, kapena mwana wa Mulungu amene

wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu kukana Mawu a Mulungu, pamene Mulungu Mwiniwake wawamasulira iwo ndikuti, “Ichi ndicho. Ine ndinalonjeza icho; ndi ichi apa,” kuwasonyeza icho mophweka mmene iwo angathere. Bwanji, iwo afika poti achipenya icho. Mwaona? Khristu angakane bwanji Mawu Ake omwe? Ngati Khristu ali mwa inu, Iye sangakane Mawu Ake omwe.

⁹³ Ndiye ife timalowa chotani mu Thupi ili? Akorinto woyamba 12, “Mwa Mzimu mmodzi ife tonse timabatizidwira mu Thupi ili,” mwa Ubatizo umodzi wa Mzimu Woyera. Ndipo izo. . . Ngati inu mukufuna kulemba izo, ndi Akorinto woyamba 12:13: “Ndipo mwa Mzimu mmodzi ife tonse timabatizidwa. . .” Ndipo Mzimu ndiwo Moyo wa Khristu (kodi nzolondola izo?), Moyo wa Khristu. Ndipo moyo wa mbewu iliyonse—chimene Iye anali Mbewu ya Mawu—umabweretsa mbewu ku moyo. Mukumvetsa izo? Ngati izo—ngati moyo umenewo wagona mu mbewu ndipo ubatizo uwu wa Mzimu Woyera nkubwera pa iyo, ifika pobweretsa moyo wa mbewu imeneyo.

⁹⁴ Monga ine ndinakuwuzirani inu kuno ku Pheonix, sikale ayi, ine ndinali kulankhula kwa M’bale John Sharriat. Ndipo ine ndinali kunjako, ndipo iye anandisonyeza ine mtengo, wa citris. Iye anali—iye amakhala ndi zipatso zambiri za citris. Ndipo iye anandisonyeza ine mtengo umodzi umene unali ndi zipatso zisanu ndi zitatu kapena zisanu ndi zinayi za mtundu wosiyana pa iwo. Ndipo ine ndinati, “M’bale Sharriat, kodi ndi mtengo wanji uwo?”

Anati, “Mtengo wa lalanje.”

Ine ndinati, “Nanga bwanji mandimuwo, ndi namchesi, ndi manyumwa, ndi mphesazo?”

Iye anati, “Zonsezo ndi zipatso za citrus; izo zamezetsanidwa.”

“O,” Ine ndinatero, “Chabwino. Tsopano, chaka chamawa iwo wonse udzakhala ndi malalanje.”

⁹⁵ “Koma, o, ayi, mtengo uliwonse udzabala zake zomwe—nthambi iliyonse idzabala chipatso chake.” Ambiri a inu olima zipatso mukudziwa izo kuno mu chigwa cha citrus; udzabala zake zomwe.

⁹⁶ Inu mukayika nthambi ya ndimu mu mtengo wa lalanje, iyo idzabala mandimu, chifukwa ndilo khalidwe la zipatso za citrus. Komabe sizingabereke za chipatso chapachiyambi. Ndipo ndi chimene ife tachita. Ife tamezetsamo, kutengeramo ndi zikhulupiriro ndi zina zotero, ndipo kumezetsanitsamo aliyense pano. Amethodisti angabale bwanji chirichonse koma mwana wa Methodisti? Chipembedzo chirichonse chingabale bwanji chirichonse koma mwana wa chipembedzo?

⁹⁷ Koma ngati mtengo umenewo ungatulutse nthambi yapachiyambi, iyo idzabala malalanje. Ndiyeno ngati Mulungu angachite chirichonse mu Mpingo, chikhala chapachiyambi kubweranso ndi Mawu limodzi chimodzimodzi. Ziyenera kutero, chifukwa moyo uli mu mtengo, ndipo iwo umabala mtundu wake womwe.

⁹⁸ Tsopano, pamene ife tikupeza... Tsopano kuti mpingo waukuluwo wayenda kupyola mu mibadwo ukubala zipatso zake, ndipo pamene nthambi zileka kubala iwo amazikhwazulapo izo. Mu Yohane Woyera 15... Samangodula mtengo tsopano, Iye anachotsa nthambizo, kuzidulapo izo, chifukwa izo sizimabala chipatso chirichonse. Ndipo—ndipo ife...

⁹⁹ Yesu akufuna chipatso cha—cha Iyemwini. Mkazi Wake ayenera kubala ana a mtundu umene Iye ali. Ndiye ngati iwo sabala ana, ana a Mkwatibwi, ana a Mawu, ndiye ndi mwana wa chipembedzo. Ndiye chikondi chake choyambirira kwa dziko ndi chipembedzo, iye wabwerera kwa icho. Ndipo iwo sangabale Akhristu enieni, osanamizira, obadwa kachiwiri, chifukwa mulibe kanthu mmenemo koti kabale izo.

¹⁰⁰ Ziri ngati, inu mukatenga nthambi ya mandimu ndikuyisomekera iyo mmenemo; iyo ibala ndimu, koma iyo siingabale lalanje, chifukwa iyo sinali pamenepo pachiyambi. Koma inadziwidwiratu pachiyambi, kuzindikiriratu kwa Mulungu kunakonzeratu iyo, ndi kunabadwa, iyo iyenera kubala lalanje basi; iyo siingabale china chirichonse.

¹⁰¹ Umo ndi momwe ziri ndi Mpingo wa Mulungu Wamoyo. Pamene ora lifika, aliyense... Muloleni Mulungu ayambe kuchita chinachake, aliyense wautenga mpira napita. Mwaona? Zakhala nthawizonse chotero. Ine ndinkawerenga mu mbiriyakale ya Marteni Lutera kuno posachedwapa. Amati kuti sizinali zovuta kwambiri kukhulupirira kuti Marteni Lutera angatsutse mpingo wa Katolika nkudutsa nazo; koma anati chinthu chachirendo, ndi kuti iye anayimitsa mutu wake pamwamba pa kutentheka konse kumene kunatsatira chitsitsimitso chake ndipo iye nkungokhalabe molunjika pa chilungamitso chake. Mwaona? Ndi chirichonse, zongowonera ndi chirichonse chogweramo...

¹⁰² Tawaonani Akazi a Semple McPherson, Aimee Semple McPherson, amene anali ndi kachisi uyu kuno. Mlaliki wamkazi aliyense anali ndi mapiko amene aja nanyamula Baibulo mofanana, kungokhala—kungokhala zochita mowonera za chithupithupi. Izo sizingakhale za pachiyambi. Umo ndi momwe mipingo siingakhale. Mpingo umodzi ungokhala ndi chinachake kapena china mu mzinda, mpingo winawo supirira mpaka iwonso ukhale nacho icho. Mwaona? Siziri za pachiyambi konse. Mawu a Mulungu ndiwo a pachiyambi. Ndi Mawu, ndipo

Iwo ayenera kubala Wake—za mtundu Wake mu nyengo Yake, osankhidwa, okonzedweratu ndi Atate Mulungu.

¹⁰³ Tsopano, ife timalowa bwanji mu Mpingo uwu? Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzili, Thupi la Khristu, limene liri Mkwatibwi, Mawu. Kubatizidwira mmenemo mwa Mzimu Woyera.

¹⁰⁴ Tsopano, tiyeni tizindikire ngati tiri mu m'badwo wotsiriza kapena ayi. Tsopano, ife tikupeza kuti ngati ife titatembenukiranso mu Genesis, cha pa, o, pafupi mutu wa 5—inu mukhoza kutembenukiranso ku Luka—ndi kupeza kuti Enoki anali wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Nowa. Enoki. . . Pamenepo pamagwiritsa mbewu ya serpenti, pakuti ngati Kaini anali mwana wa Abele, ndiye iye anali wachisanu ndi chitatu. Mukuona? Koma palibe pena mu Baibulo pamene ananena kuti Kaini anali mwana wa Abele—kapena Kaini—kapena Kaini anali mwana wa Adamu, chifukwa kuti Baibulo linati iye anali wa woyipayo. Ndipo Adamu sanali woyipayo. Mwaona? Iye anali wa woyipayo.

¹⁰⁵ Tsopano, ife tikupeza apa kuti Enoki anali wa chisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Nowa chimene chinali choyimira mibadwo ya mpingo. Tsopano, amuna asanu ndi mmodzi onse aja asanadze iye anafa, koma Enoki anasinthidwa, Enoki anakwatulidwa, wa chisanu ndi chiwiri, kusonyezera kuti ndi M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri umene ukutenga mkwatulo. Tsopano, palibe zokayikitsa kuti ife tiri mu M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri. Ife tonse tikudziwa izo.

¹⁰⁶ Tsopano, ndi M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri umene ukutenga mkwatulo. Ena asanu ndi mmodzi aja anafa. Koma Enoki anasinthidwa chifukwa iye sanapezeke; Mulungu anamutenga iye. Koma Enoki anakwatulidwa, zinali zoyimirira ena onsewo kufa, koma—Mkwatibwi wa nthawi yotsiriza adzayitanidwa kuchokera mu (kukwatula, opanda kufa)—adzayitanidwa kuchoka mu M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri. Umene ife tiri nawo tsopano umboni wake wa m'badwo umenewo. O, mai! Tiyeni tikumbe mkati tsopano mwakuya zedi. Mwaona?

¹⁰⁷ Tsopano, panonso mthunzi wa Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri, imene mu Chivumbulutso 10:7 kuti chinsinsi chachikulu cha Bukhu chinali choti chidzawululidwe ndi Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri.

¹⁰⁸ Tsopano, pamakhala Mtumiki pamwamba nthawizonse, ndipo mtumiki pa dziko lapansi. Liwu la Chingerezi loti *mngelo* limatanthawuza “mtumiki.” Ndipo mu Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri, pamene iye ankapanga kwake—kufalitsa utumiki wake, ndiye pamene iye akuyamba kufalitsa utumiki wake, osati pamene iye ankayamba. . . Yesu pamene Iye ankayamba, Iye anayamba ndi kuchiritsa odwala ndi

osautsidwa. “Ndipo o, Rabbi wotchuka uyo, Iye ndi mneneri!” Ndipo aliyense anamufuna Iye mu mpingo Wake, koma pamene Iye anakhala pansi tsiku lina nati, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi,” izo zinali zosiyana. Izo zinali zosiyana. “Ndipo ngati simudya thupi la Mwana wa munthu ndi kumwa Magazi Ake, mulibe Moyo mwa inu.” Bwanji, Ameneyu ndi mfiti.” Onani, mwaona? Izo zinali zosiyana. Iye sanafotokoze izo. Iwo anali atawona kale makwaniritsidwe, kutsimikizirika kwa Mawu a Mulungu a kwa m’badwo Wake atapangitsidwa kukhala enieni natsimikizidwira kwa iwo kuti Iye anali Mtumiki wa m’badwo umenewo. Ndipo Iye sanasowe kufotokoza kalikonse.

¹⁰⁹ Ophunzira amenewo mwina samakhoza kufotokoza izo, koma iwo anazikhulupirira izo ngakhale iwo akanakhoza kufotokoza izo kapena ayi. Iwo anangokhala mosatekeseka nakhulupirira izo. Iwo akanadziwa bwanji ngati akanati azidzadya thupi Lake ndi kumwa Magazi Ake? Bwanji, zinali zosatheka kuti iwo atero, koma iwo anakhulupirira izo, chifukwa iwo anali okonzedweratu. Yesu anati Iye anawasankha iwo dziko lapansi lisanakhazikitsidwe. Mwaona? Iwo anazikhulupirira izo. Kaya iwo akanakhoza kufotokoza izo kapena ayi, iwo anakhulupirirabe izo.

¹¹⁰ Tsopano, yang’anani! Tsopano, mu M’badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri pamene mngelo wa chisanu ndi chiwiri akuyamba kuwomba, zinsinsi za Mulungu zinali zoti zikadziwike pomwepo. Zisindikizo zimene okonzanso... Akanati asakhale kuti anali ndi nthawi... Lutera sanakhale moyo motalika kokwanira, ngakhaleso Wesile, mibadwoyo siinakhale nthawi yaitali kokwanira. Okonzansowo, iwo anali ndi uthenga wawo wa tsiku limenelo, ndipo anthu anawugwira iwo napanga nawo chipembedzo. Ndi chiyani ichi?

¹¹¹ Inu simungagonjetse chirengedwe. Chirengedwe nthawizonse chimachitira umboni. Mulungu amayendetsa mogwirizana ndi chirengedwe. Ziyenera kuteru. Monga dzuwa, dzuwa limatuluka m’mawa; ndi kamwana kakang’ono kabadwa. Ndi kofooka, kalibe kutentha kokwanira mwa iko. Teni koloko, kutsiriza sukulu yapamwamba. Pakati pa tsiku, akuyamba kulowa m’moyo. Firii koloko madzulo, wayamba kukalamba. Faii koloko, akufa, wokalamba ndi wofookanso, kubwerera ku manda. Kodi uko ndi kutsiriza kwake? Limawukanso m’mawa winawo. Mwaona?

¹¹² Yang’anani pa mitengo momwe iyo imakhalira ndi masamba ake, chirichonse chimene iyo imachita. Tsopano, ife tikupeza kuti masamba amathothoka mu mtengo, nabwerera. A... Chiyani? Moyo umapita pansi ku mizu ya mtengo. Kodi kutha kwake ndi kumeneko? Umabwereranso nyengo yina ya kuphukira kwa masamba ndi moyo watsopano.

113 Tsopano, yang'anani mipingo, momwe iyo yachitira chinthu chomwecho mukukonzanso. Iyo inaphuka. Mbewu ya tirigu ija inagwera mu nthaka niifa pansi pa chisautso cha mu M'badwo wa Mdimu. Iyo inapita pansi. Inayenera kufa. Munthu aliyense wauzimu akhoza kuwona zimenezo. Pokha mbewu imeneyo ikafa niivunda, iyo imangokhala yokha. Ndipo inayenera kupita pansi mu M'badwo wa Mdimu. Iyo inagona mmenemo, inavunda, niutulukira mwa timasamba tiwiri ta Mpingo wa Luterani. Kuchokera mwa mpingo wa Luterani munaturuka masamba ochuluka, Zwingli ndi ena otero. Kuchokera pamenepo kudzafika popanga ngayaye, zimene anali Joni Wesile, m'badwo wopambana wa utumwi. Izo zinaweramira mmbuyo. Kuchokera mmenemo munadza m'badwo wonyenga uja, m'badwo wa Chipentekoste uja. Mbewu ya tirigu ija, imene . . .

114 Alipo wina aliyense muno amene anabzala tirigu? Kamuyang'anani tirigu ameneyo. Pamene inu mumuyang'ana uyo . . . Pamene inu mupita kunja uko ndi kukati, "Ine ndiri ndi tirigu." Mukuwoneka ngati muli ndi tirigu mmenemo; mtseguleni iye mwatcheru ndikumuyang'anansitsa, inu mulibe tirigu nkonse. Muli ndi mankhusu. Kodi Yesu sanatichenjeze ife izo mu Mateyu 24:22–24, mu masiku otsiriza kuti mizimu iwiri idzakhala yoyandikana kwambiri iyo ikanadzanyenga tirigu wosankhidwa yemwe ngati kukanakhala kotheka. Mwaona? Tsopano yang'anani, ndi chongonyamulira.

115 Tsopano, Moyo umene unadza kupyolera mwa Lutera ndi umene unapanga Wesile. Moyo umene unachokera mwa Wesile ndi umene unapanga Pentekoste. Moyo umene ukuchokera mu Pentekoste ukupanga tirigu. Koma iwowo ndi zongonyamulira. Mwaona? Moyo weniweniwo ukupita kupyolera mmenemo. Uthenga wangopita kupyolera mwa iwo, koma tsopano ukunka kokakhala tirigu amene. Icho ndi chifukwa chomwe tirigu akudza nadzakwatulitsa chinthu chonsecho pamwamba apa. Mkwatibwi yemwe wachokera mu m'badwo uliwonse, koma phesi la zipembedzo limafa, limawuma ndipo limafa.

116 Kodi inu mwawona mmasiku otsirizawa momwe zayambira kukanganukira tsopano? Pamene tirigu akuyamba kukula, ndiye—mankhusu amayamba kukanganuka kwa iyo. Kayang'aneninso mu tirigu wamng'onoyo inu mukadzamuwona uyo. Katseguleni chonchi ndi kuyang'anamo kuti muwone; inu muli ndi kamphukira kakang'ono ka mbewu ya tirigu kumbuyoko. Mungasowe kutenga galasi lokulitsa zinthu makumi atatu kuti mukawone kamphukira ka tirigu kumbuyo uko. Mwaona? Koma ndi mkatimo, koma iko kamayamba kukula. Tsopano, mankhusu ayenera kukakhala mmenemo kuti azitetezera iyo kuyipatsa iyo mwayi kuti ituluke. Komano pamene iyo iyamba kukula ndipo Uthenga uyamba kufalikira, ndiye mankhusu amakanganuka kwa iyo. Ndipo moyo

umachoka mwa nkhusuyo kukalowa mu tirigu. Kumapitirira. Umo ndi momwe m'badwo uliwonse umachitira. Izo chabe—izo sizingagonjetse chirengedwe konse; ndi. . . Uko ndi kupitiriza kwa Mulungu, momwe Iye amachitira zinthu. Ndipo tsopano, umenewo ndi m'badwo womwe ife tikukhalamowu pakali pano, M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri.

¹¹⁷ Tsopano, zonsezi ndi zoti zikwaniritsike mu mbewu ya tirigu potsiriza. Kubwereranso kwina. . . Tsopano, ngati mutatenga Luka mutu wa 17 ndi ndime ya 30, Iye anati, “Monga momwe zinaliri m'masiku a Sodomu, zidzakhala chimodzimidzi pa kudza kwa Mwana wa munthu, pamene Mwana wa munthu adzayamba kudziwulula Yekha.” Kuwulula ndi chiyani? Kupanga vumbulutso Lake la chomwe Iye ali mu tsiku ili, kuwululidwira kwa anthu, Mawu amene adziwika lero, kuwululidwira kwa anthu mwa chikwaniritso cha Mzimu Woyera, kumupangitsa Yesu kukhala wamoyo pakati pathu.

¹¹⁸ Ndipo kumbukirani, Iye ankayimiridwa kuja mwa Munthu, Mwamuna, Iye anati, “Monga kunali.” Tsopano, Iye ankawerenga Baibulo lomwe tikuwerengali, Genesis. Tsopano, ife tikuwona kuti mu mutu wa m'Genesis umo pamene Yesu anali kulankhula za izi. . . Ife tikupeza mmenemo kuti Iye atalozetsa nsana Wake ku hema uyo, ndi Sara mkati mwa hema, Iye anati—Iye anafunsa funso. Ndipo iye sanakhulupirire za zomwe amati zidzachitikazo kuti zingachitike. Iye anati, “Tsopano, Abrahamu, ine ndidzakuchezetsa iwe mwa nthawi ya moyo.” . . . ? . . . Ndipo Sara ali mu hema anaseka za izo. Iye anati, “Chifukwa chiyani Sara anaseka mu hema, nati, ‘Zinthu izi zingatheke bwanji?’” Yesu analonjeza, ndipo uja anali Iye; Abrahamu anamutcha Iye, *Elohim*, Wamphamvuzonse. Ujayu anali Iye.

¹¹⁹ Tsopano, Baibulo limalosera kuti izo zidzabwereranso mu tsiku lotsiriza. Yesu anatero. Ndipo pamene inu muwona zinthu izi zikuyamba kuchitika, ingokumbukirani, pamene izi zikuyamba kuchitika chotero, ndiye ndi—inu mudziwa kuti nthawi yayandikira pakhomo.

¹²⁰ Yang'anani dziko palokha. Yang'anani dziko, Sodomu ngati kunali Sodomu. Yang'anani anthu, kusokonezedwa mu chisokonezo chotero. Malingaliro awo asokonezeka. Iwo sakudziwa kuti khalidwe labwino ndi chiyani. Yang'anani kusamvera malamulo, kugonana kwa amuna, ndi zina zirizonse. Yang'anani akazi athu, chisokonezeko chanji chapangidwa. Yang'anani chisokonezeko cha makhalidwe, chiwerewere pakati pa akazi athu, osati pakati pathu pokha. . . Inu mukuti, “Amenewo ndi Achimethodisti.” Amenewo ndi Achipentekoste nawo. Ndi chinthu chonse.

¹²¹ Yang'anani pa amuna athu; iwo amakanirira. . . Mmalo mwa Mawu a Mulungu, timiyambo tina tating'ono ta chipembedzo

timene iwo akukangamirako mmalo mwa kutuluka pamene iwo akuwona Mulungu akudzidziwitsa Yekha mwangwiro. Chifukwa chimene, iwo ali akhungu, ndipo sangawone izo. Iwo sadzatha kuziwona izo.

Tsopano, penyani zimene zikuchitika pano mu izi, pamene ife tikufulumira. Ine ndikuganiza kuti mayi uyo akufuna ife kuti titulukemo muno; ine ndamuona iye akusonyeza ndi manja ake, chinachake kapena chinzake cha zimene iye akufuna kuti ife titulukemo, kotero ife tingofulumira.

¹²² Kotero tsopano, zindikirani Enoki, woyimira Mpingo. Apa iye akuyimiridwanso mu M’badwo wa Mpingo Wachisanu ndi chiwiri. Kodi inu mungaganizire za izo? M’badwo wa Mpingo Wachisanu ndi chiwiri. . . Zindikirani, pa kuwomba kwa . . .

¹²³ Ndi ngati amene akukhulupirira kuti kunali atumiki asanu ndi awiri kwa isanu ndi iwiri. . .? O, ife tonse tikukhulupirira izo ngati kuti ife tikukhulupirira Baibulo. Ngati ife sitikukhulupirira Baibulo, chifukwa (mwaona?) ife sitikukhulupirira iwo. Koma analipo. . .

¹²⁴ Tsopano, ife tikukhala mu M’badwo wa Mpingo Wachisanu ndi chiwiri. Ndipo pamene Baibulo linati kuti M’badwo uwu Wachisanu ndi chiwiri. . . Pamene mtumiki wa Mpingo Wachisanu ndi chiwiri ayamba kufalitsa Uthenga wake, kuti zinsinsi za zinthu zonse zimene zapotolezedwa popyola mu mbadwo zidzawululidwa mu nthawi imeneyo. Ndipo pano tikuziwona izo, Mwana wa munthu akudza pakati pa anthu Ake ndi kuchita chimodzimodzi, kutsimikizira Uthenga Wake monga momwe Iye ananenera kuti Iye adzachita. Pano ife tikupeza izi mu m’badwo wotsirizawu.

¹²⁵ Tsopano. . . Ndipo alonda asanu ndi awiri, monga alonda asanu ndi awiri nthawi yina. . . Iye sanabwere pa nthawi ya mlonda woyamba, wachiwiri, wachitatu, wachinayi, koma anabwera pa nthawi ya mlonda wachisanu ndi chiwiri. Ameneyo anali Enoki, wachisanu ndi chiwiri, amene anasinthidwa, ndipo Nowa, pokhala woyimira otsalira Achiyuda, adzanyamulidwira uko.

¹²⁶ Tsopano, mu nthawi ya Baibulo—pokamba za alonda—ndipo usiku sunkagawidwa mu maora mu nthawi za Baibulo. (Tsopano mverani mwatcheru, pakuti ndifulumirirapo tsopano chifukwa iwo akufuna mchipinda chino). Ayi, Baibulo silinali logawidwa—kapena usiku siunali wogawidwa mu maora mu nthawi ya Baibulo; iwo unagawidwa mu ulonda.

¹²⁷ Panali ulonda utatu. Tsopano, ulonda woyamba umayamba pa—kuyambira 9:00 mpaka 12:00; ulonda wachiwiri umayambira 12:00 mpaka 3:00, ndipo ulonda wachitatu wa usiku unali kuyambira 3:00 mpaka 6:00. Tsopano, ife tiri ndi atatu, ma atatu atatu, zomwe ziri zisanu ndi zinayi, nambala yosakhala yangwiro. Ndiye ife tibwerera ku yachisanu ndi

chiwiri chifukwa cha mkwatulo, umene uti udzachitike ine ndikukhulupirira pakati pa 6:00 ndi 7:00—kapena 6:00 ndi 9:00 mmawa wina. Pakuti lipenga la Ambuye lidzalira . . .

Mmawa wowala wopanda mitambo pamene akufa mwa Khristu adzawuka,
 Ndi kugawana ulemerero wa chiwukitsiro Chake;
 Pamene osankhidwa Ake adzasonkhana kupita kwawo kuseri kwa thambo,
 Akamadzayitana mayina kutsidyako, ine ndidzakhala komweko.

¹²⁸ Liwu lakuti *mkwatulo* mu Baibulo silimagwiritsidwa ntchito konse. Ife tinangoliyikapo liwu limenero pamenepo. Baibulo limati, “Kukwatulidwa mmwamba, kukwatulidwa mmwamba.” Ife timawerenga apa mu 2 Atesalonika kapena 1 Atesalonika kani, dongosolo la mkwatulo waukuluwo umene uti udzachitike mu masiku otsiriza. Mverani izi apa. Ife tiyambira apa ndi ndime ya 13.

“...Ine sindifuna kuti inu mukhale...osadziwa, abale, pokamba za iwo amene akugona, kuti inu musalire, monga enawo amene alibe chiyembekezo.

Pakuti ngati ife tikukhulupirira...Khristu anafa nawukanso, koteronso ngakhale iwo...amene agona mwa Yesu Mulungu adzabwera nawo palimodzi naye.

Pakuti...ife tikunena ichi kwa inu mwa Mawu a Ambuye, kuti ife amene tiri ndi moyo otsalirafe mpaka pa kufikanso kwa Ambuye, sitidzawalepheretsa... (kapena liwu loti sitidzawalepheretsa likutanthawuza “sitidzawatsekereza.”)...iwo amene akugona.

Pakuti Ambuye mwiniwake adzatsika...(Tsopano, mverani mwacheru)...

...Ambuye mwiniwake adzatsika kuchokera kumwamba ndi mfuu, ndiponso ndi liwu la mngelo wamkulu, ndi...lipenga la Mulungu: ndipo akufa mwa Khristu adzayamba kuwuka:”

¹²⁹ Tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire chinthu chopambana chikuchitika apa tsopano. Musachiphonye ichi. Mwaona? Tsopano zindikirani, Mawu akutero apa mu 11 Atesalonika kuti pali zinthu zitatu...Zindikirani, kuyambira pa 13 mpaka ndime ya 16 pali zinthu zitatu zimene ziyenera kuchitika Ambuye Mwiniwake asanatulukire. (Mofulumira tsopano kuti ife tikhoze kutseka. Mukuona?) Chinthu choyamba kuchitika, zindikirani: mfuu, liwu, lipenga. Tiyeni tiwerenge izo tsopano tiwone ngati ziri zolondola. Mwaona?

*Pakuti Ambuye mwiniwake... (ndime ya 16)...
adzatsika kuchokera kumwamba ndi mfuu, ndipo ndi
liwu la mngelo wamkulu, ndi... lipenga la Mulungu:...*

¹³⁰ Zinthu zitatu kuchitika, liwu—mfuu, liwu, lipenga, ziyenera kuchitika Yesu asanawonekere. Tsopano, *mfuu*. Yesu akuchita zonse zitatu pamene Iye—Iye—Iye akutsika. “Mfuu,” “mfuu” ndi chiyani? Ndi Uthenga pamene ukulalikiwa choyamba, Mkate wa Moyo umene ukubweretsa Mkwatibwi.

¹³¹ Tsopano, Mulungu ali ndi njira yochitira zinthu, ndipo Iye sasintha dongosolo Lake. Iye sasintha Zake... Iye ndi Mulungu wosasintha. Mu Amosi 3:7 Iye anati Iye sangachite kanthu pa dziko lapansi Iye asanayambe wawulula icho kwa antchito Ake aneneri. Ndipo moonu basi monga Iye analonjezera icho, Iye adzachichita icho.

¹³² Tsopano, ife tapyola mu mibadwo ya mpingo, koma ife tinalonjezedwa mu masiku otsiriza malingana ndi Malaki 4 kuti padzakhala kubwereranso, mneneri mu dziko. Izo nzolondola! Zindikirani khalidwe lake ndi mmene iye ati adzawonekere. Iye ndi... O, iye... Mulungu akugwiritsa ntchito Mzimu umenewo kasanu: kamodzi mwa Eliya, mwa Elisha, ndi Yohane Mbatizi, kuwutulutsa Mpingo, ndi otsalira a Ayuda; Kasanu, grace, J-E-S-U-S, f-a-i-t-h, [Mawu awa li ndi zilembo zisanu mu chingezezi kutanthawuza chisomo, Yesu, chikhulupiriro—Mkonzi.] ndipo ili nambala ya chisomo. Mwaona? Chabwino.

¹³³ Tsopano kumbukirani, Uthenga walonjezedwa. Ndipo pamene zinsinsi zonsezi zamangidwa mitolo ndi ziphunzitsa za zipembedzo, zitengera—mneneri wochokera molunjika kwa Mulungu kuti awulule izo. Ndipo ndi momwemo zimene Iye analonjeza kuti achite. Mwaona?

¹³⁴ Tsopano kumbukirani, Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri, osati kwa wophunzira zaubusa, mneneri. Iye ndi wonyezimiritsira Mawu a Mulungu. Iye sanganene kanthu; iye sanganene maganizo ake omwe; iye akhoza kungolankhula chomwe Mulungu akuwulula. Ngakhale kwa mneneri Balamu pamene iye ankayesa kudzigulitsa—kugulitsa ufulu wake; iye anati, “Mneneri aliyense anganene bwanji chirichonse kupatula chimene Mulungu ayika mkamwa mwake?” Ndi chinthu chimene Mulungu akuchita chomwe iwe siunganene china chirichonse. Ndipo iwe unabadwa chotero.

¹³⁵ Mosaposa momwe iwe unga... Ngati iwe ukanati, “Ine—sindingatsegule maso anga,” pamene iwe ukuyang’ana. Mwaona? Iwe ukhoza. Iwe siungathe kufikira dzanja lako pamene ukhoza. Mwaona? Iwe siungakhale galu pamene uli munthu. Mukuona? Iwe unapangidwa chotero basi, ndipo Mulungu wachita nthawizonse ku—mmibadwo yonse ya Yesaya, Yeremiya, ndi—ndi onse—Eliya, ndi mibadwo yapitayo, pamene magulu azipembedzo amakhoza kusokonezeka zinthu zonse, Iye

amakhoza kutumiza mneneri, kumudzutsa iye kuchokera kosadziwika. Iye ndi woti asakhale wa za mzikhalidwe zawozo, nalankhula Mawu Ake, nachotsedwapo napita, munthu uyu wolimba wa Choonadi cha Mulungu.

¹³⁶ Ndipo nthawizonse ndi... Momwe inu mukanamudziwira iye, Iye anati, “Ngati akhalapo wina pakati panu amene ali wauzimu kapena mneneri...” Tsopano mneneri... Pali chinthu chonga mphatso ya uneneri mu tchalitchi, koma mneneri ndi wokonzedweratu ndi kuzodzedweratu kwa ora’lo. Mwaona? Inde, bwana!

¹³⁷ Tsopano, ngati ulosi uchitika, awiri kapena atatu ayenera kukhalapo naweruza ngati zinali zolondola kapena ayi, mpingo usalandire izo. Koma palibe amene angayime pamaso pa mneneri, chifukwa iye anali—iye anali mwamtheradi Mawu a Mulungu. Iye anali Mawu amenewo mu m’badwo wake. Iye anawona Mulungu akunyezimiritsa...

¹³⁸ Tsopano, ngati Mulungu analonjeza kuti atitumizirensa ife ameneyo mu masiku otsiriza kuti adzatulutse Mkwatibwiyo kuchokera mu chisokonezeko cha zipembedzocho, ndipo izo... Njira yokha yomwe zingachitikire. Sizidzachitika konse... Mpingo siungamulandire Khristu. Ife... Achipentekoste, ife sitingapitirire ndi Uthenga uwu momwe mpingo ulirimu lero. Ife tingapitirire chotani mu nthawi yotsiriza mu chikhalidwe chimene iwo alimo lero, pamene aliyense akusutsana ndi mzake, ndi china chirichonse, ndi mwachipembedzo? O, chifundo. Ndi nyansi. Zapitiratu mu zipembedzo. Ndi nthawi iliyonse, ine ndikufunsa wa za mbiriyakale aliyense kuti—kuti—kuti anene chosiyana. Nthawi iliyonse pamene uthenga umafalitsidwa mu dziko lapansi ndipo pamene iwo amawupangira bungwe iwo, iwo umafera ndipwepo. Ndipo Pentekoste yachita chinthu chomwecho monga iwo onse... Pentekoste imene yatuluka...

¹³⁹ Inu a Assemblies of God, pamene abambo anu oyamba ndi amayi anu anatuluka mu mabungwe amenewo kalelo mu General Council yakaleyo, anafuula nayamikira Mulungu nalankhula motsutsa zinthu zimenezo; ndipo inu munapotoloka ngati garu ku masanzi ake ndi nkhumba kumatope ake ndi kuchita chinthu chomwecho chimene iwo anachita; ndipo tsopano kungokhala a chipembedzo kwambiri inu mukutsekereza chifundo cha mkati mwanu, ndipo uyenera kukhala ndi khadi la chiyanjano asanayanjane nanu mpang’ono konse.

¹⁴⁰ Ndipo inu a umodzi, Mulungu anakupatsani inu uthenga chotero, ndipo mmalo moti mupitirire nawo ndi kumangodzichepetsa ndi kupita patsogolo, munalekerera ndi kupanga bungwe gulu lanu. Ndipo tsopano muli patino? Mu chidebe chomwecho. Ndi momwemo! Ndipo Mzimu wa Mulungu

ukupitirira. “Ine Ambuye ndidzabzala; Ine ndidzathirira iwo usana ndi usiku kupangira kuti wina angadze. . .”

¹⁴¹ Iye anakonzeratu zinthu izi kuti zidzakhalepo, ndipo Iye ayenera kutumiza ichi. Chinthu choyamba kudza pamene Iye akuyamba kutsika kuchokera Kumwamba, kuli mfuu! Ndi chiyani icho? Ndi Uthenga wowabweretsa anthu palimodzi. Uthenga ukudza choyamba. Tsopano, “Ndi nthawi yokonza nyali. Dzukani nimukonze nyali zanu.” Unali ulonda uti umenewo? Wachisanu ndi chiwiri, osati wachisanu ndi chimodzi, wachisanu ndi chiwiri. “Onani Mkwati akudza. Dzukani nimukonze nyali zanu.” Ndipo iwo anatero. Ena a iwo anapeza kuti analibe ngakhale mafuta mu nyali zawo. Mwaona? Koma ndi nthawi yokonza nyali. Ndi nthawi ya Malaki 4 pamene mukudza. . . Ndi Luka 17. Ndi—ndi Yesaya. . . Mauneneri onse aja kuti zikhoza—kuyika zinthu zonse mwangwirowo mwa dongosolo kwa tsiku ili mu Malemba, ife tikuziwona izo zikukhala momwemo. Palibe. . .

¹⁴² Kuwona zinthu izi zikuchitika, M’bale wanga wokonedwa, Mlongo, pamene Mulungu Kumwamba akudziwa kuti ine ndikhoza kufa pa nsanja iyi pakali pano, inu—mungoyenera kuyenda chozungulira pang’ono. Ine. . . Zangokhala. . . Ndi zopambana. Pamene inu mukuwona Mulungu akudza kuchokera Kumwamba, kuyima pamaso pa magulu a anthu, nayima pamenepo, kudziwonetsa Yekha monga momwe Iye ankachitira. . . Ndipo icho ndi Choonadi, ndipo Baibulo ili liri lotsegula. Mwaona? Ife tafika!

¹⁴³ Ndipo dongosolo la zipembedzo ndi lakufa. Ilo lapita. Ilo silidzadzukanso. Lidzawotchedwa. Izo ndi zomwe inu mumachita ndi mankhusu kumunda. Thawani kwa izo. Kaloweni mwa Khristu. Musati, “Ine ndine wa Methodisti”; “Ine ndine wa Baptisti!”; “Ine ndine wa Chipentekoste!”; Inu mulowe mwa Khristu. Ndipo ngati inu muli mwa Khristu, palibe liwu limene lalembedwa umu koma limene inu mumalikhulupirira. Sindikusamala zimene wina aliyense akunena. Ndiyeno Mulungu amapangitsa chinthu icho kuwonetsereka, chifukwa inu. . . Pamene Iye atsanulira Mzimu Wake pa Mawu, chimachitika ndi chiyani? Monga ngati kuthira madzi pa mbewu ina iliyonse. Ikhala ndi moyo, ndipo ibala za mtundu wake.

¹⁴⁴ Inu mukuti, “Ine ndiri ndi ubatizo wa Mzimu Woyera.” Izo sizikutanthawuza kuti iwe wapulumutsidwa, ayi kutalitali ndithu.

¹⁴⁵ Tayang’anani kuno, inu ndinu chinthu cha patatu. Inu muli. . . Mkati mwa kamunthu aka muli moyo; chotsatira ndi mzimu; ndipo chotsatira ndi thupi. Tsopano, inu muli ndi mphamvu zisanu mu thupi ili kuti muzikhudzira nyumba yanu ya pansu pano. Izo sizimakhoza kuzindikira zonse za izo. Inu

muli ndi mphamvu zisanu za mzimu mkatimu, chikondi ndi chikumbumtima ndi zina zotero. Koma mkatikatimu ndi momwe inu mumakhalamo. Ndi chomwe inu muli.

¹⁴⁶ Kodi Yesu sanati mvula imagwera pa olungama ndi osalungama omwe? Ikani chisoso apa, ndi tirigu apo, ndi kusanulira madzi pa izo, ndi kuzithirira fetereza ndi zinthu zotero, kodi zonsezo sizikhala moyo mwa madzi omwewo? Zedi! Koma ndi chiyani? Wina wa iwo adzabzala chisoso, chifukwa ndicho chonse chimene iye ali. Chisoso, chidzakweza manja ake nichifuula chimodzimidzi ngati tirigu.

¹⁴⁷ Kodi Baibulo silimanena kuti mmasiku otsiriza kudzabwera akhristu abodza, osati a Yesu abodza tsopano, akhristu abodza, odzozedwa, odzozedwa mwabodza kwa Mawu. Odzozedwa kwazipembedzo koma osati kwa Mawu, pakuti Mawu adzadzichitira Okha umboni. Iwo sasowa china chirichonse; Iwo adzadzichitira Okha umboni. Ndipo kudzabwera odzozedwa mwabodza. Inu muli nayo tepi yanga pa izo. Ndipo kudzoza uko. . . O, ngati mukanamuyitana wina ndi kuti, “O, inu—kodi ndinu Yesu?”, “O, ayi ndithu!” Iwo sakanakhoza kuyimira izo. Koma pamene ziti zibwere pakuti, “O ulemerero, ine ndiri ndi kudzoza. . .” Ndipotu ndi kudzoza kwenikweni.

¹⁴⁸ Kumbukirani, Kayafa anali nakonso ndipo ananenera. Chimodzimidzinsu Balamu anali nako nanenera, koma izo ziribe chochita ndi chomwe chiri mkatimu. Pokha imeneyo ikanakhala mbewu ya Mulungu, khalidwe Lake kuchokera pachiyambi, okonedweratu, inu mwatha. Ine sindikusamala kuti umafuula chotani, kulankhula ndi malirime, kuthamanga, kufuula; zimenezo ziribe chochita ndi ichi. Chisoso chikhoza kuwerenga chimodzimidzi ndi momwe ena onsewo. Ine ndawawonapo achikunja akunyamuka, nafuula, nalankhula mmalirime, ndipo—namwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu, namamuyitana mdierekezi. Mwaona? Kotero inu simukufuna zirizonse za zotengeka ndi zinthu; iwalani izo. Ndi mtima wanu mu Mawu, ndipo iwo ndi Khristu. Alowetseni iwo mmenemo, ndipo yang’anani Iwo akudzidziwitsa Okha monga pamene Iwo akungotsegukira monga mbewu yina iliyonse ndi kuzidziwitsa Okha kwa m’badwo womwe Iwo akukhalamo.

¹⁴⁹ Lutera sakanadza ndi kalikonse koma timphukira. Izi zina zikanadzabweretsa zinthu zinazi. Ife tiri mu m’badwo wa tirigu tsopano. Aluterani, Aluterani enieni anayenera kubala Lutera weniweni. Pentekoste yeniyeni inayenera kubala Pentekoste yeniyeni. Ndi zomwezo. Koma ife tapyola m’badwo umenewo ndipo tikupitirirabe.

¹⁵⁰ Inu mukudziwa mpingo wa Katolika unayambitsa Chipentekoste? Ndipo ngati mpingo wa Chipentekoste ukanayima zaka zikwi ziwiri, ukanakhala monyansa kusiyana ndi momwe Katolika aliri tsopano. Ndi momwemo! Tsopano,

ine ndikunena izi kwa abale anga ndi alongo anga amene ine ndimawakonda, ndipo Mulungu akudziwa izo. Koma kumbukirani, amzanga, ine ndiyenera kudzakumana nanu kutsidya pa chiweruzo. Ndipo ilo mwina silingakhale kale kwambiri. Ine ndiyenera kuchitira umboni chimene chiri Choonadi.

¹⁵¹ Pamene ine ndinapita mmisonkhano ndi inu kupempherera odwala, zinali zabwino, koma pamene ine ndikudza ndi Uthenga. . . Ngati uthenga uliwonse ufika, ngati uli uthenga woona, ngati uli woona, zozizwitsa zenizeni za Mulungu, ndipo nangokangamira mu bungwe lomwelo, inu mudziwa kuti si wa Mulungu, chifukwa chinthu chimenecho chawonetsedwa kale. Yesu anapita nakachiritsa odwala ndi cholinga choti akope maso a anthu, kenakono Uthenga Wake. Izo nzolondola! Uwo uyenera kukhala ndi chinachake chimene Mulungu ati ayambitse. Iye akungo. . . Machiritso Auzimu ndi. . . Zozizwitsa monga izo zimangokopa maso a anthu. Mtima wake wa izo ndi Uthenga. Apo ndi pamene pali. Ndi chomwe chikuchokera mkatimu. Iye akuyesa kupeza chiyanjano ndi anthu kuti iwo akhoze kukhala namumvera Iye. Mwaona? Pakuti pali ena muno amene ali odzozedwera ku Moyo. Ndipo mbewu zina—tirigu anagwera pa nthaka, ndipo mbalame zinadzazitola izo. Ndi zina zinagwera pa minga, ndipo zina ndi—zinapita pa nthaka yokonzedwa kale, nthaka yokonzedwa kale, nizibala.

¹⁵² Ayi, ndi. . . Chinthu choyamba ndi kuwomba—kapena kuti chinthu choyamba ndi lipenga ndi—kapena liwu—mfuu, ndiye liwu, ndiyeno lipenga. Mfuu, mtumiki kuwapangitsa anthu kukhala okonzeka. Chachiwiri ndi liwu la chiwukitsiro. Liwu lomwelo limene, liwu lofuula mu Yohane Woyera 11:38 ndi 44 limene linamuyitana Lazaro kuchokera mmanda. Kubweretsa Mkwatibwi palimodzi, ndipo kenako chiwukitsiro cha akufa (mwaona?), kuti akwatulidwe nawo palimodzi. Tsopano, penyani zinthu zitatu zikuchitika.

¹⁵³ Chotsatira ndi chiyani? linali lipenga. Liwu—mfuu, liwu, lipenga. Tsopano, chinthu chachitatu ndi lipenga, chimene nthawizonse pa Phwando la Malipenga ndi kuyitanira anthu ku phwando; ndipo umenewo udzakhala mgonero wa Mkwatibwi mmwamba, mgonero wa Mwanawankhosa ndi Mkwatibwi mu mlengalenga.

¹⁵⁴ Mwaona, zinthu zoyamba kudza ndi Uthenga Wake kuyitana Mkwatibwi palimodzi. Chinthu chotsatira ndi chiwukitsiro cha Mkwatibwi wogona,—amene anafa mmbuyomo m'mibadwo ina. Iwo akudzakwatulidwa palimodzi, ndipo lipenga, phwando mmiyamba—mu mlengalenga. Bwanji, ndi—ndicho chinthu chomwe chiti chidzachitike, amzanga.

¹⁵⁵ Ife tiri pamenepo kumene okonzeka tsopano. Chinthu chokha, Mpingo umene ukutuluka uyenera kukhala pamaso pa

dzuwa kuti ukhwime. Chophatikiza chopambana chibwera kuno pakangopita kanthawi. Tirigu—adzawotchedwa, mapesi, koma mbewu zidzasonkhanitsidwira mu nkchokwe yake. Mwaona?

¹⁵⁶ Inu sindinu anthu akhungu. Inu ndinu—ndinu anthu oganiza bwino, ndipo ngati ine ndikanayima pano ndikunena zinthu zimenezo mokondera. . . Ine ndikuzinena izi chifukwa ndi Moyo, chifukwa ine ndidzayankha kwa Mulungu chifukwa chozinena izo. Ndipo ine ndiyenera ndizinene izo. Ndipo Uthenga wanga. . . Nthawi zonse kudziwa kuseriko pa machiritso ndi zina zotero, kunali kungowakopa anthu, kudziwa kuti Uthenga udzabwera. Ndipo ndi uwu.

¹⁵⁷ Ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo zinatsegula, zinsinsi zija ndi kuwonetsa zinthu zimene zija kuti ndi zomwe zinachitika. Ine sindinkazidziwa izo, koma pali mwamuna amene wayima ndi ine pakali pano amene anayima nane pamene inu nonse munandimva ine ndikulalikira ulaliki uja woti, *Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino?* Ndipo mmawa umenowo penipeni pamene ananena kuti zidzachitika, panadzayima Angelo asanu ndi awiri akungochokera Kumwamba. Ndipo pamene iwo anapita mmwamba, ndipo kamvuluvulu uja anawatenga iwo kupita mmwamba muja, ife titayima, kumayang'ana pamene iwo anali kupita kutali, sayansi inajambula chithunzi chake mu mafuko onse a dzikoli, mpaka komwe ku Mexico. Ndipo kumeneko pamene ine ndinali ndikuyang'ana. . .

¹⁵⁸ Tsiku lina pamene ine ndinayamba kulalikira mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo iyi, ndipo ine ndinamuyitana Jack Moore, wodziwa Mawu wotchuka; ine ndinati, “Jack, Ndi ndani Munthu uyu amene akuyima pamenepo, Pali Wina wonga Mwana wa munthu, amene wayima pamenepo tsitsi loyera ngati ubweya.” Ine ndinati, “Iye anali Mwamuna wamng'ono; Iye angakhale bwanji ndi tsitsi loyera ngati ubweya?”

¹⁵⁹ Iye anati, “M'bale Branham, limenelo linali thupi Lake la ulemenero.” Izo sizinalize belo. Koma pamene ine ndinapita mchipinda ndi kukayamba kupemphera, Iye anandirola ine kudziwa chomwe chinali.

¹⁶⁰ Onani, ine nthawi zonse ndakhala ndikulalikira kuti Iye anali Umulungu, osati munthu chabe; Iye anali Mulungu atakwaniritsika mu thupi, Mulungu, Lingaliro la Mulungu la chikondi, Malingaliro opambana amene anadza nawonetsera pansi pano za Mulungu. Yesu anali chikondi cha Mulungu, chimene chinamanga thupi limene Yehova Mwiniwake anadzakhalamo. Iye anali chidzalo cha Umulungu mu thupi. Chomwe Mulungu anali, Iye anachikwaniritsa kupyolera mu thupi limenelo. Thupilo linayenera kufa kotero kuti Iye akamtsuke Mkwatibwi ndi Ake—ndi Ake—ndi Magazi Ake.

¹⁶¹ Ndipo zindikirani, osati kokha kuti Mkwatibwi watsukidwa, kukhululukiridwa, koma kuti walungamitsidwa. Mwaona? Kodi inu munayamba mwayesa liwu loti *kulungamitsidwa* kuti muwone chomwe likutanthawuza? Tsopano mwa chitsanzo, ngati M'bale Green akanamva kuti ine ndimamwa, ine ndimachita zinthu zoyipa, ndiye iye nadzazindikira kuti ine sindinachite izo, ndiye iye nabwera, nati, "Ine ndakukhululukirani inu, M'bale Branham."

¹⁶² "Inu mwandikhululukira ine? Ine sindinazichite izo. Inu mukundikhululukira ine chiyani?" Mwaona? Koma ngati ine ndalakwa, ndiye ine ndikhoza kukhululukiridwa, koma ine sindine wolungama, chifukwa ine ndinazichita izo. Koma liwu loti *wolungamitsidwa* ndi kuti "ngati siunazichite konse"—wolungamitsidwa. Ndiyeno Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife ku machimo, mpaka kuti ayikidwa mu bukhu la Mulungu la zoyiwalidwa. Iye ali Yekha amene angachite zimenezo. Ife sitingatero. Ife tikhoza kukhululukira, koma osayiwalira.

¹⁶³ Ine ndikhoza kukhululukirani inu, koma ine nthawizonse ndidzakhala ndikukumbukira inu kuti munachita zinthu zoyipa izi. Ndiye inu si wolungama, inu mwakhululukidwa. Koma pamaso pa Mulungu Mkwatibwi ndi wolungamitsidwa. Iye sanazichite izo kuyamba nkuyamba. Amen. Kuyima pamenepo wokwatiwa kwa Mwana wa Mulungu wolemekezekayo, sanachimwe kuyamba nkuyamba. Bwanji? Iye anakonedweratu; Iye anakodwera mu ichi. Ndipo tsopano pamene Iye anamva Choonadi nabwera, Magazi anamuyeretsa Iye. Ndipo Iye akuyima pamenepo wolemekezeka. Mwaona? Iye ndi. . . Wopanda tchimo pa iye konse.

¹⁶⁴ Kotero, Uthenga ukuyitanira Mkwatibwi palimodzi. Mwaona? Mfuu ndi lipenga. Yemweyo wa liwu lomveka Iye anafuula ndi mfuu umenewo, ndi—ndi liwu ndipo anamudzutsa Lazaro. Ndi liwu lomveka Iye anafuula, "Lazaro, dzuka." Mwaona? Ndipo liwu limadzutsa—limadzutsa Mkwatibwi wogona, ogona mwakufa.

¹⁶⁵ Ndipo lipenga, ndi kumveka kwa lipenga, ndipo pamene litero, ilo limayitana. . . Nthawizonse lipenga linkayitanira Israeli ku Phwando la Malipenga (mwaona?), limene linali phwando la Pentekoste, phwando lopambana mu mlengalenga ndipo Phwando la Malipenga. . . Ndipo tsopano, lipenga linkalengeza za kuyitana palimodzi, kuyitanira ku phwando. Ndipo tsopano limenelo ndi la—mgonero wa Mwanawankhosa mu mlengalenga (tsopano, penyani,)—kusonkhana palimodzi mwa Mkwatibwi, Phwando la Malipenga, Mgonero wa Chikwati.

Ife tawuona iwo mu mithunzi. Tsopano, penyani mphindi chabe tisanatseke.

¹⁶⁶ Zindikirani, ife taziona izo mwa mithunzi. Tsopano, ngati inu mukufuna kuwerenga mu Mateyu 18:16, anati, pali zitatu zimene zimachitira umboni. Mwaona? Mu—1 Yohane 5:7 ndi ena otero. . . Zitatu nthawizonse ndi mboni. Si choncho? Ndi chitsimikiziro, chinachake chimene chiri cholondola. Mboni zitatu zimene zikuyimira. . . “Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu mulole mawu aliwonse akhazikike.”

¹⁶⁷ Tsopano zindikirani, ife takhala ndi mboni zitatu. Zitatu ndiye mboni. Tsopano, ife takhala ndi mikwatulo itatu kale mu Chipangano Chakale (kodi inu mumadziwa izo?) monga mboni. Tsopano penyani! Enoki anali mmodzi; Eliya anali wina; ndipo Yesu anali winanso. Yesu, pokhala Mwala womangiriza tsopano, Iye anachitira umboni. Onani, Iye anali Mwala womangiriza pakati pa Chakale ndi Chipangano Chatsopano, chifukwa Iye poyamba anayenera kufa ndiyeno mkwatulo. Iye anafa, nakhala moyo, nayendayenda kuno ndi ife, ndiyeno anakwatulidwa; chifukwa Iye anali Mwala womangiriza umene unadzamangiriza ziwirizo palimodzi. Chiwukitsiro Chake chitachitika ndi mkwatulo (onani!), Iye atachita zimenezo natsimikizira kuti Chipangano Chakale uko. . . Iye tonse tikudziwa Enoki anakwatulidwa. Iye tikudziwa kuti Eliya anatengedwa mmwamba ndi kamvuluvulu (sichoncho?) pa galeta la moto. Ndipo Yesu anafa, kuyikidwa, kuwuka nakhala moyo pansu pano ndiyeno anakwatulidwa, Mwalawomangiriza. Pali atatu woti achitire umboni. Sichoncho?

¹⁶⁸ Tsopano, kwakhala kale mkwatulo umodzi wapita kale. Kodi inu mumadziwa izo? Lolani—tiyeni tiwone ngati ife sitingaziwerenge izo mofulumira ndithu. Tiyeni tipeze Mateyu mutu wa 27, ndipo tiyeni tipeze, pafupi, ndime ya 45 ya Mateyu mutu wa 27. Tiyeni tiwone ngati ife sitingapeze pamene mofulumira ndi kuwona ngati ife sitingapeze pang’ono chabe pamene pangatithandize ife mofulumira—27 ndi 45 ine ndikukhulupirira kuti ndinalamba apa. Tiyeni tiwerenge.

“Tsopano kuyambira ora lachisanu ndi chimodzi panali mdima pa dziko lonse mpaka lachisanu ndi chinayi. . .

Ndipo litayandikira ora lachisanu ndi chinayi Yesu analira ndi liwu lofuula, nati, Eli, Eli, Lama, sabakatani? ndiko kunena kuti, Mulungu Wanga, . . . inu mwandisiyiranji ine?

Ena a iwo amene anayima pafupi, . . . anamva izo, ndipo anati, Munthu uyu akuyitana. . . Eliya.

Ndipo nthawi yomweyo mmodzi wa iwo anathamanga, nakatenga chinkhupule, nachidzaza icho ndi vinyo wosasa, nachiyika icho pa bango, nachipereka icho kwa iye kuti amwe.

Ena onse anati, . . . tiyeni ife tiwone ngati Eliya ati abwere nadzamupulumutsa.

Yesu, pamene iye analira . . . ndi liwu lofuula, anapereka . . . (Liwu lofuula, liwu lofuula, onani, pamene Yesu anali kufa analira ndi liwu lofuula.) . . . napereka mzimu.

Ndipo, tawonani, chinsalu cha mkachisi chinang'ambika pawiri kuchokera pamwamba mpaka pansi; ndipo dziko linagwedezeka, ndi miyala inasweka;

Ndipo manda anatseguka; ndipo matupi ambiri a . . . oyera amene anagona anawuka,

Ndipo anatulukuka mmanda pambuyo pa kuwuka kwake, napita mu mzinda woyera, nakawonekera kwa ambiri."

169 Mkwatulo umodzi wapita kale. Itatu inachitika mu Chipangano Chakale ya iwo amene anali okonzeka amene Mawu a Ambuye anadza kwa iwo. Mwaona? Mawu a Ambuye anadza kwa Enoki. Mawu a Ambuye anadza kwa Eliya. Iye anali mneneri. Mwaona? Mawu a Ambuye anali Yesu. Mwaona?

170 Yang'anani mu Chipangano Chakale, oyera mtima a Chipango Chakale aja tsopano pamene mkwatulo uwu unachitika koyambaka. Onani ndime ya 50: Liwu Lake lofuula linadzutsa oyera a Chipangano Chakale chimodzimidzi ndi momwe liwu lofuula linamudzutsira Yesu—kapena linamudzutsa Lazaro. Mwaona? Liwu lofuula linadzutsa. Ndipo kachiwiri ukukwaniritsidwa mu 2 Atesalonika mutu 4. Tiyeni tingowerenga—kuwerenga . . . Ife tinangowerengapo maminiti angapo apitawo. Mwaona? "Ine sindikufuna inu kuti mukhale osadziwa, abale, pokamba za ogonawo, kuti inu musadandaule, ngakhale . . ." Uyo ndi 1 Atesalonika 4:12-18. Kuti—uwo udzakhala mkwatulo wachiwiri. Mkwatulo wachiwiri udzakhala kupita kwa Mkwatibwi.

171 Oyera a Chipangano Chakale anapita mpaka Pamaso Pake, paradiso anathetsedwa. Ndipo Oyera a Chipangano Chakale anakwera mmwamba, liwu Lake lofuula litamveka pamene Iye analira napereka Mzimu. Chifukwa chiyani? Nsembe, chitetezero cha machimo awo chimene iwo anali kuchiyembekezerera . . . Kukhulupirira kuti Mwanawankhosa wangwiro anali kudza, iwo anali akuti akapereke nsembe ya mwanawankhosa. Ndipo pamene Iye anafa napereka Mzimu, Iye analira ndi liwu lofuula, ndipo Oyera a Chipangano Chakale anawuka. Penyani mfuu ndi liwu pamenepa, chimodzimidzi pa kudza Kwake. Mwaona? Anapereka Mzimu, ndipo pamene Iye anatero nsembe inali yangwiro, ndipo paradiso anasesedwa; ndipo Oyera a Chipangano Chakale anadza pa dziko kachiwiri, anayenda padziko lonse, nalowa mkati ndi Iye pa mkwatulo Wake.

172 Davide anatero uko, “Tsegulani, inu zipata zosatha, nimunyamulidwe mmwamba.”

173 Iye anatsogolera undende akundende napereka mphantso kwa anthu. Pamene oyera a Chipangano Chakale anakalowamo palimodzi ndi Iye, iwo anati, “Mfumumu ya chilungamo iyi ndi ndani?”

174 “Ambuye wa ulemerero, wamphamvu mu khamu—khamu lamphamvu.” Apa iwo anadzalowa, akuguba. Yesu anatsogolera undende akundende. Ndipo apa Iye akudza ndi oyera a Chipangano Chakale, ndipo—analowa mu zipata zatsopano mmwambamo, nati, “Tsegulani, inu zipata zosatha, nimunyamulidwe mmwamba, ndipo lolani Mfumumu ya ulemerero ilowe.”

Liwu linamveka kuchokera mkatimo, kuti, “Mfumumu ya ulemerero ndi ndani?”

175 “Ambuye, wamphamvu mu nkondo.” Zipata zinatseguka. Ndipo Yesu Mgonjetsi anatsogolera undende akundende iwo amene anamukhulupirira Iye, ndipo Mawu anadza kwa iwo. Kumeneko oyera a Chipangano Chakale atakhala mmenemo akuyembekezera. Iye anatsogolera undende akundende, anakwera mmwamba, anatenga oyera a Chipangano Chakale nalowamo. Mkwatulo umodzi wachitika kale.

176 Mkwatulo wachiwiri ukuchitika ndiwo II Atesalonika kwa Mpingo, Mkwatibwi, kudzawukitsidwa kukwatulidwira mu ulemerero. “Ife amene tiri moyo ndipo tatsalira (ndiro thupi lomwe latsalira pansu pano) sitidzalepheretsa kapena kutsekereza iwo amene akugona; pakuti lipenga la Mulungu lidzalira koyamba, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka. (Mwaona?) Ndipo ife amene tiri moyo ndipo tatsala tidzakwatulidwa kupita mmwamba palimodzi nawo.”

177 Tsiku lina ine ndinali nditayima pa ngodya ya msewu, ndipo ine—ndinali nditayima pa—ndinali nditayima pa ngodya ya msewu ndi kuwonera kuguba kwa Tsiku la Ankhondo. Ndipo pamene anapitirira, akukwera ndi msewu, ine ndinayima pamenepo ndi mwana wanga wamng’ono Joseph. Kunabwera—oyamba anali akasinja akale a nkondo yoyamba akubwera, ti akasinja takale. Atatha amenewo anabwera akasinja a Sherman a nkondo yatsopano ndi mifuti yaikulu ndi mipope yotulukira zipolopolo itawomberedwa ndipo—mpope wosweka pa mfutizo ndi zina zotero. Atatha amenewo kunabwera asirikali, a—a—amayi a nyenyezi ya golide. Ndiyeno kunabwera zonyamulidwa ndi—konseko. . . Ndipo konseko kunali zonyamulidwa, ndipo patsogolo pakepo panali manda a msirikali wosadziwika; ndipo pamenepo panayima—msirikali atayima pamenepo, mlonda wa pa manda. Pamenepo panayima wa mnyanja pa mbali ina, ndi woyendetsa panyanja pa mbali inayo. Ndipo panali kugawaniza komwe kunachitidwa, ndipo pa mbali inayo kunali mayi

anali wa nyenyezi ya golide. Iye mnyamata wake anamwalira. Pamenepo panayima mkazi wake wamng'ono mutu wake uli pa tebulo akulira, ka mnyamata kakang'ono katavala nsanza katakhala pambalipo, ndipo misonzi ikuyenderera pa nkhope yake, abambo ake anamwalira. Ine ndinaganiza, “Zomvetsa chisoni bwanji, pamene ine ndayima pano kuyang'ana, kuwawona akalewo—atangotsala asirikali pang'ono chabe, akuguba pansipo opunduka ndi okalamba, chotero, ndi yunifolomu zawo, koma monyadira kuwonetsera izo, chifukwa iwo anali Achimereka.”

¹⁷⁸ Ine ndinaganiza, “O, Mulungu wanga, tsiku lina kudzabwera lipenga kuchokera Kumwamba, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka koyamba. Oyera aku Chipangano Chakale aja amene akuyembekezera kulizako kuchitike natulukamo poyamba ndi kupita mu chiwukitsiro; ife tidzagwera mu mzerewo ndikupita mu mlengalenga, matupi akale achivundiwa atasinthidwa napangidwa monga thupi Lake la ulemerero lomwe. Ndi—ndi kuguba kwa mtundu wanji kumene kuti kudzakhalepo pamene udzayamba wa kumwamba tsiku linali mu nthawi ya mkwatulo imene ili mtsogolomu, o, monyadira kuwonetsera Magazi a Yesu Khristu pa zifuwa zawo, Uthenga wa Mulungu mu ora limene iwo anakhalamo. Ndiro ora limene ife tikuliyembekezera, m'bale.

¹⁷⁹ Yang'anani (potsiriza chabe tsopano), chiwukitsiro chachiwiri, onse—choyamba chinachitika. Chachiwiri chayandikira pakali pano, chidzafika—chiri pafupi tsopano.

¹⁸⁰ Tsopano, chachitatu ndi mboni ziwiri za Chivumbulutso 11:11 ndi 12, amene iwowa ndi amene akubwerera ndi Mzimu wa Khristu kudzachitira umboni kwa Ayuda monga momwe Yosefe anachitira kwa abale ake. Ndipo inu mukukumbukira mitembo yawo yakufa inagona mu misewu kwa masiku atatu ndi theka; ndiye mzimu wa moyo unadza mwa iwo ndipo iwo anakwatulidwa, kutengedwa kupita Kumwamba. Ndi imeneyo mikwatulo yanu itatu ya mu Chipangano Chatsopano. Mikwatulo itatu ya Chipangano Chakale, yonseyo inapita.

¹⁸¹ Tsopano, ife tiri okonzeka, kudikira mikwatulo—mkwatulo wa oyera. Zinanenedwa ndipo kotero zidzachitika.

¹⁸² Pamene Mulungu anena chirichonse, miyamba yonse ndi dziko zidzachoka, koma Mawu amenewo sadzalephera konse. Mulungu anati mmbuyo muja ku Genesis 1, Iye anati, “Kuwale” . . . Zikhoza kukhala zaka mazana kuwalako kusanakhalepo. Iye anati, “Kukhale mtengo wa mgwalangwa; kukhale mtengo wa chiwale; kukhale chipululu; kukhale phiri; kukhale *ichi*.” Iye anachitchula icho. Mukuona? Ndipo bola kuti zinachokera pakamwa pake mwa mawu, zinayenera kukwaniritsika. Ziyenera kutero. Pamene . . .

183 Ndiye tsiku lina Iye anayitana anthu ake kuti atuluke, ndipo Iye analankhula kwa munthu wotchedwa Mose mwa Lawi Lamoto, Kuwala, Moto woyera, wopatulika. Ndipo Mose sakanakhoza . . . Anthu sakanamukhulupirira Mose, kotero Iye anati, “Kabwere nawo mpaka ku phiri ili.”

184 Mmawa umenewo phiri lonse linadzaza ndi moto, ndi ziphaliwali, ndi mabingu, chotero, ndipo anthu anati, “Musamulole Mulungu kuti alankhule; msiyeni Mose azilankhula (mwaona?), kuwopa kuti tingawonongeke.”

185 Mulungu anati, “Ine sindidzalankhula nawonso chotero, koma ine ndidzawautsira iwo mneneri. Ndipo ine ndidzalankhula kupyolera mwa iye, ndipo ngati chimene iye alankhula chichitika ndiye inu mumvere izo, chifukwa Ine ndiri—Ine ndiri ndi iye.” Tsopano, Iye analankhula izo. Iye anati kuti zidzachitika.

186 Yang’anani pa mneneri uyu Yesaya atayima pamenepo, mwamuna, mwamuna wanzeru, mwamuna amene anali woganiziridwa bwino ndi mfumu, chifukwa iye ankakhala ndi Uziya mfumu, amene anali munthu wotchuka. Anayesa kutenga malo a mlaliki nthawi ina nakalowa mkati, anakanthidwa ndi khate. Ndi zimene ine ndinawawuza Anthu a Bizinesi. Musayese kutenga malo a mlaliki. Ayi, bwana! Inu mukhale pomwe mulipo. Mwaona? Inu muzichita ntchito yanu, imene Mulungu anayiyika—anakuwuzani inu. Ngati inu muli chala, inu simungakhale khutu. Ngati inu muli khutu, simudzakhala mphuno, mphuno kapena diso. Mwaona? Inu khalani mmalo anu.

187 Inu munamvera Uthenga tsiku lina ukuwulutsidwa. *Kuyesa Kumchitira Mulungu Ntchito*. Davide mfumu yodzozedwa, anthu onse akufuula ndi kukweza mawu kuti zinali bwino, koma iye anali asanafunse mneneri wa Mulungu. Ndipo munthu anafa, ndipo chinthu chonse chinadetsedwa. Musamayesere kumchitira Mulungu ubwino. Inu muyembekezere mpaka zitakhala mwa kuchita kwa Mulungu. Siyani izo zibwere mwa njira Yake yochitira izo. “Ine ndiyamba chinthu chachikulu ichi, icho chidzachita *ichi*.” Samalira, m’bale.

188 Tsopano, Davide amadziwa bwino koposa izo, Natani anali mu dziko tsiku limenelo. Iye sanafunsidwe nkomwe. Mwaona? Iye anafunsira kwa woyang’anira wa mazana ndi zikwi. Anthu onse anafuula nalira ndi kuvina ndipo . . . ? . . . Iwo anali ndi kutengeka konse kwa chipembedzo, koma sizinali mu mzere ndi dongosolo la Mawu a Mulungu, ndipo izo zinalephereka. Chinthu chirichonse chimene sichiri mu mzere ndi dongosolo la Mawu a Mulungu chidzalephera. Mawu a Mulungu okha adzayima kwa nthawizonse. “Miyamba ndi dziko zidzachoka koma osati Mawu Anga.”

189 Zindikirani Yesaya, mnyamata uja wanzeru atayima pamene. Mwakamodzi Mzimu unamukhudza iye. Iye sakanalankhula mosiyana, iye anali mneneri. Iye anati, “Taonani, namwali adzayima. Kwa ife Mwana wamwamuna wabadwa—Mwana wabadwa, Mwana wamwamuna wapatsidwa. Dzina Lake adzatchedwa Wauphungu, Kalonga wa mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha. Matsiriziro a Iye... Ulamuliro udzakhala pa phewa Lake...?... Sipadzakhala chitsiriziro kwa ulamuliro Wake.” Munthu ameneyo anganene bwanji mwanzeru kuti namwali adzayima? Aliyense nkumayembekezera icho. Chalankhulidwa kale; chinali PAKUTI ATERO AMBUYE. Chinayenera kudzachitika, chifukwa anali Mawu a Mulungu omwewo amene anali mu Genesis pamene Iye anabzala mbewu pansu pa nyanja, pamene ilo linali lopanda mawonekedwe ndi mdima, ndipo madzi anali mwakuya. Mwaona, zinayenera kudzachitika.

190 Ndipo tsiku lina patapita zaka mazana asanu ndi atatu mimba ya namwali inabala Mbewu ya Mulungu, Mbewu yolengedwa. Iye anabala Mwana wamwamuna. Mwana wamwamuna yemweyo anayima pamene tsiku lina ndipo Iye anati, “Lazaro, dzuka.” Ndipo munthu amene anali atafa masiku anai atavunda, mphuno yake italowa, akununkha; iye anatuluka. Anati, “Musadabwe pa ichi, pakuti ora likudza (amen!) pamene onse amene ali mmanda adzamva Liwu la Mwana wa Mulungu.” Koterono zinalankhulidwa kale; ziyenera kuchitika. Padzakhala mkwatulo.

191 O, mai! ine ndikukumbukira chabe uthenga wanga wotsiriza mu California kumene ine ndimaganza kuti sindidzabwereranso, pamene ine ndinalosera za Los Angeles kuti adzamizidwa pansu pa nyanja yaikulu. Ndipo PAKUTI ATERO AMBUYE, zidzachitika! Iye wathedwa; iye wakokoledwa; iye wathedwa. Ora lanji? Ine sindikudziwa liti, koma iye adzamizidwa. Zitangotha izo zivomezi zinayamba kugwedeza ndi kuchuluka.

192 Inu mukukumbira, ambiri a anthu inu mutayima pomwepo, mwala uja tsiku lija pamene Mngelo uja anatsika kumeneko ndipo Kuwalako ndi Moto zikugwa kuchokera Kumwamba pozinga mwalawo pamene ife tinali titayima pamene, miyala ikuponyeka kuchokera ku phiri, ndi kumagwera cha kumeneko. Ndipo anaphulitsa katatu molimba; ine ndinati, “Chiweruzo chikantha Gombe la Kumadzulo.” Masiku awiri izo zitachitika Alaska anali pafupi kumizidwa.

193 Kumbukirani, Mulungu yemweyo amene ananena izo, anati Los Angeles wathedwa. Ndipo iye watha. Ine sindikudziwa kuti ndi liti; ine sindingakuwuzeni inu.

194 Ine sindinadziwe kuti ine ndinanena izo. Koma m’bale uyu pano ine ndikukhulupirira anali...Ayi, mmodzi wa a

Mosely, ine ndikukhulupirira, anandiyitanira ine panja pa msewu kumeneko. Ine sindimadziwa kuti ndi chiyani mpaka ine nditayang'ana mmbuyo. Ndipo ine ndiyang'ananso mu Lemba, ndipo Yesu anati, “Kaperna, Kaperna, kochuluka chotani. . . Iwe wadzikweza wekha (kani) mpaka Kumwamba udzatsitsidwa pansu kukalowa ku gehena, pakuti ngati ntchito zamphamvu zinali zitachitidwa mwa iwe—izo zikanachitidwa mu Sodomu, akadakhala alipobe lero.” Ndipo pafupi zaka zana ndi makumi asanu kuchokera pamenepo—Sodomu anali kale mu nthaka—ndiye Kaperna nayenso ali mmadzi lero.

¹⁹⁵ Ndipo mzimu womwewo wa Mulungu umene unalankhula zinthu zonsezi, nuchita zinthu zonsezi, Iwo unati pomwepo, “O mzinda, Kaperna, amene umadzitcha wekha ndi dzina la angelo, Los Angeles. Momwe wadzikwezekerwa wekha mpaka Kumwamba. (Muzu ndi mpando wa Satana umene. Mwaona?) Iwe wadzikweza wekha.”

¹⁹⁶ Alaliki, ndiwo manda a iwo. Amuna abwino amapita kumeneko nakafa ngati makoswe. Kuwononga kotani.

¹⁹⁷ “Iwe amene umadzitcha wekha ndi dzina la angelo, ngati ntchito zamphamvu zikanachitidwa mu Sodomu zimene zachitidwa mwa iwe, bwenzi alipo lero. Koma ora lako lafika.” Inu mupenye ndikuyembekeza. Ngati sichoncho, ndine mneneri wabodza. Mwaona? Ndi ameneyotu, iye akugona apo.

¹⁹⁸ Ine ndikukumbukira usiku uja. . . Ine ndisanawone icho, ine ndinawona chiwonetsero cha Mkwatibwi. Ine ndinayima apo ndipo ndinawona mkazi wamng'ono wokongola wovala mwabwino ndi zinthu akugubira cha uku. Panali Wina atayima pafupi ndi ine mmasomphenya, ndipo ine ndinawona iwo akuti, “Chiwonetsero cha Mkwatibwi.” Ine ndinamuwona Iye akudutsa. Iwo amabwera mbali iyi nayenda chozungulira.

¹⁹⁹ Ndipo ine ndinamva iwo ukubwera; m—mpingo unali ukubwera mbali inayi. Panabwera mpingo wachi Asia. O, mu kunena za uve. Apa pakubwera mpingo waku Ulaya. O, mai! Ndiyeno ine ndinamva gwedemula akubwera; ndipo uyo anali Abiti America, mpingo. Ndipo iye analibe zovala zirizonse. Iye anali ndi pepala, ngati nyuzipepala, yotuwirapo, atagwira kutsogolo kwake, akuvina gwedemula—Abiti America mpingo.

²⁰⁰ Ine ndinayima pamenepo mkukhalapo Kwake. Ine ndinaganiza, “O, Mulungu, monga mlaliki, ngati izo ziri zopambana zimene tachita, o, o!” Inu simukudziwa momwe ungamvere. Ndiye ine ndinaganiza, “Mulungu ndibiseni ine; ngati ine ndikanangochokapo pano. Ngati zonse zimene ife tazichita, ndipo izo ndi zimene ife tapindula, ngati izo ndi zomwe. . .”

²⁰¹ Ndiyeno pamene akazi amenewo anapyola, onse akuchita zochita za mitundu yonse za gwedemula ndi zinthu, ndi tsitsi lalifupi, ndi nkhope zopentedwa. Ndipo pamene iwo

anali kupyolapo chotero, oyenera kukhala anamwali kwa Khristu...Ndipo pamene iye anali kupyola chotero...ine ndinatembenuza mutu wanga, inu mukudziwa ndi ichi... Kumangochiwonetsabe patsogolo panga; chinali—ndi zopanda ulemu, kumbuyo kwawoko. Ndipo kumeneko iwo anali akupita chotero.

²⁰² Ndipo ine ndinatembenuza mutu wanga ndikulira chotero. Ine ndinati...Ine—sindikanatha kupirira izo pamenepo, Iye atayima pamenepo, ine ndikudziwa kuti ndine mtumiki wa mpingo ndipo izo ndi zomwe ndinapindulira kwa Iye. Ine ndinati, “O, Mulungu, ine sindingamayang’ane pa izo. Ndiroleni ndife. Ndiroleni ine—ndiroleni ine ndiyiwalike,” ndi monga choncho.

²⁰³ Ndipo pamene anangochoka—nthawi iliyonse mmodzi wa iwo amakhoza kubwera, iwo amakhoza kupita ku malo ena ake nakagwera kumeneko, ndipo ine ndimangomva phokoso lake pamene amapita kutali. Ndiyeno ine ndinamva chinachake chomveka ngati *Tiyeni Patsogolo Asirikali Achikhristu*. Ndipo ine ndinayang’ana, ndipo kunadza gulu lija la tiasungwana oyera chimodzimodzi basi momwe anali, onse ovala bwino, tsitsi lawo likugwera pansu chakumbuyo kwawo, bwinobwino, awukhondo, akuguba chotere mwa sitepe ya Uthenga. Iye anali Mawu. Ndipo ankawoneka ngati mmodzi kuchokera ku fuko lirilonse. Ine ndinali kuwayang’ana pamene anali akupyola apa, ndi kuwawona iwo akupyola apa. Mmalo mopita pansu, iwo anayamba kupita mmwamba. Ndipo ine ndinazindikira mmodzi wa iwo akuyesa, awiri kapena atatu a iwo akuyesa—kuchoka mu mzere; ine ndinafuula, “Khalani mu mzere!” Ndipo masomphenya anandichokera ine, ndipo ine ndinali nditayima mu chipinda ichi ndikufuula, “Khalani mu mzere!” Mzere umene... .

²⁰⁴ Kudabwa, kodi zingakhale zitachitika kale? Kodi Mkwatibwi angakhale atayitanidwa kale? Kodi izo ndi zomwe tikupyolamo lero? Iye ayenera kuwumbidwa ndi kupangidwa mwa chifaniziro cha Khristu, ndipo Khristu ndi Mawu. Ndi chinthu chokhacho. Onani, ziri mkatimo, mu Mawu, zangokhala... .Onani, sipangakhale kanthu kamodzi kowonjezedwa. Sangakhale—mkazi wokhala ndi—dzanja limodzi ngati mwamuna ndi linzake lokhala ndi mkono monga galu; ziyenera kukhala chimodzimodzi Mawu a Ambuye, monga momwe Iye ali Mawu. Mkwatibwi ndi gawo la Mkwati. Mkazi ndi gawo la mwamuna wake, chifukwa iye anatengedwa kuchokera kwa mwamuna. Eva anali gawo la Adamu kuchokera mu mbali yake. Ndipo chotero ali ndi Mkwatibwi, osakhala wotengedwa kuchokera mu zipembedzo, koma wotengedwa kuchokera mu chifuwa cha Mawu a Mulungu a tsiku ili.

²⁰⁵ Mkwatulo:

Lipenga la Ambuye lidzalira;
 Akufa mwa Khristu adzawuka,
 Ndipo ulemerero wa Chiwukitsiro Chake
 adzagawana;
 Pamene osankhidwa adzasonkhana kumka
 kwawo kuseri kwa thambo,
 Pakuitana mayina kutsidyako . . .
 (Tiyeni tonse tiyesetse tikakhale kumeneko,
 amzanga.)

²⁰⁶ Mulungu akudalitseni. Zalankhulidwa; ziyenera kufika pochitika. Izo zidzafika pochitika! Ndipo anthu aang'ono, palibe mmodzi akufuna kufa; palibe mmodzi akufuna ku—kuti atayike. Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu, chirichonse chomwe inu muchita, ine sindikusamala momwe mukuchitira bwino popita ku tchalitchi ndi momwe mukukhalira wodzipereka ku tchalitchi. . . Izo nzabwino; palibe chotsutsa izo; inu muyenera kumapita ku tchalitchi. Inu muzichita izo; zipitanibe ku tchalitchi, koma kaya ndi chiyani, tayani miyambo yanu ndi kumapitirirabe mpaka mwa Khristu; chifukwa kudzamveka limodzi la masiku awa, ndipo inu mudzagwidwa ndi chilembo cha chirombo pa inu ndi kusadziwa chomwe chiri mpakana nthawi itatha. Izo nzolondola kumene!

²⁰⁷ Mulungu akudalitseni. Pepani ndakukhazikani inu. Ndipo kumbukirani, ine ndawayimika iwo nthawi yaitali kuno; izo nzolondola. Ndipo chopereka chimene munanditengera ine, chimene ine sindimakufunsani inu kuti mutero. M'bale. . . Umenewo ndi wanga. . . Umenewo ndi ulemu. Tengani izo ndipo mulipirire motel'yi—nthawi yowonjezerayi, chifukwa ndi ineyo amene ndinayitenga. Ine ndinangokhala ndi zinthu pang'ono apa. Ine ndidakali ndi masamba asanu ndi atatu kapena khumi owonjezera pa mkwatulowo apo, koma ine—ine ndinangokhala opanda nthawi yoti ndizipereke izo.

²⁰⁸ Mulungu akudalitseni inu! Kodi mumamukonda Ambuye Yesu? Tiyeni tingoyima nji kwa miniti chabe tsopano, mwakachetechete, mwaulemu. Ndipo kumbukirani zimene ine ndanena. Kumbukirani, ife tiri mu maora otsiriza. Izi. . . ?

Mafuko akusweka;
 Israeli akuwuka;
 Zizindikiro zomwe Baibulo linaneneratu:
 Masiku a Amitundu akwanira ndi zowopsya
 zachuluka.
 Bwererani, o Omwazika, kwanu.

Tsiku la Chiwombolo layandikira;
 Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha.

Dzazidwani ndi Mzimu,
 Nyali zanu konzani ziwale.

Yang'anani mmwamba, chiombolo chanu
chayandikira. (Inu mukudziwa izo?)

Aneneri onyenga akunama;
Choonadi cha Mulungu akuchikana; (Ife
tikudziwa zonsezi ndi zowona, sichoncho?)

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye,
Chifukwa Iye anayamba kundikonda,
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

²⁰⁹ Ndi angati amene akumukonda kumene Iye, kwezani dzanja lanu. Tsopano, ine ndikufuna inu, pamene ife tikuyimbanso nyimboyi, gwiranani chanza ndi wina wake ali pafupi, ndikuti, “Mulungu akudalitseni inu, mwendamnjira!” Ife ndi a mwendamnjira sichoncho, a mwendamnjira ndiponso alendo?

Ndimkonda Iye, (Ndi choncho, kwa amene ali
mbali yina ya tebuloyo). Ndimkonda Iye,
Chifukwa Iye anayamba kundikonda,
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

²¹⁰ Inu mukufuna mudzakhoze kukwatulidwa? Ndi angati amene ali okondweretsedwa kuti adzakwatulidwe, itini, “Mulungu, ine ndikufuna kudzapita ndi mtima wanga wonse.”

Gwirani Pa Dzanja Losasinth la Mulungu. Mukuidziwa nyimboyi? Inu mukuidziwa, Mlango? *Gwirani Pa Dzanja Losasinth la Mulungu.* Ine sindikudziwa chiyani. . . Kodi muli chiyani umo. . . ? . . . Ndi chiyani. . . Aa?

Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!
Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!
Manga chiyembekezo chako pa zinthu za
muyaya,
Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!

Mukuikonda imeneyo?

Pamene ulendo wathu udzatha,
Ngati kwa Mulungu wakhala woona,
Kwabwino ndi kowala kwanu ku ulemerero,
Moyo wako wokwatulidwa udzawuona!

Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!
Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!
Manga chiyembekezo chako pa zinthu za
muyaya
Gwira pa dzanja losasinth la Mulungu!

Ine ndikufuna inu muweramitse mitu yanu kwa kamphindi chabe tsopano.

Usakhumbire chuma chabe chamdziko,
 Chofulumira kuvunda,
 Funa kupindula chuma cha mmwamba,
 Icho sichidzatha konse!


Gwira pa dzanja losasintha la Mulungu!
 Gwira pa dzanja losasintha la Mulungu!
 Manga chiyembekezo chako pa zinthu za
 muyaya,
 Gwira pa dzanja losasintha la Mulungu.

²¹¹ Tsopano, mitu yanu itaweramitsidwa ndipo ichi chiri mmalingaliro, podziwa kuti ife tikuweramitsa mitu yathu ku fumbi komwe tinachokera, tsiku lina tidzabwerera; kudziwa kuti muli ndi moyo mkatimo umene uyenera kudzayankha kwa Mulungu...Ndipo ngati inu mukumva kuti inu simunakonzekere chabe mkwatulowo, mwakuti ngati ukanadza usiku uno, ndipo inu mukufuna kukumbukiridwa mu pemphero, ingokwezani dzanja lanu. Ife tiribe malo kuti tiyitanire ku guwa. Guwa lanu liri mu mtima wanu basi. Kwezani dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu. Mai! “Ndikumva ngati sindiri wokonzeka, M’bale Branham. Ine—ine—ndikufunadi ine—ine ndikufuna kukhala Mkhristu. Ine ndayesa kukhala, koma nthawizonse pali chinachake chikusowa. Ine—ine ndikudziwa kuti ine—ine sindiri kumene ndinayenera kukhala. Ndimvereni chifundo, Mulungu. Ine ndakweza dzanja langa, khalani wachifundo kwa ine.” Tsopano, manja ena makumi awiri kapena atatu akhala atakwera kale mu kagulu aka kakang’ono. Ambiri akukwerabe.

²¹² Wokonedwa Mulungu, Inu mukudziwa chomwe chiri paseri pa dzanjalo mkati mwa mtimawo. Ine ndikupemphera, Mulungu wokonedwa...Pali chinthu chimodzi chokha chomwe chiri ntchito yanga, ndicho kunena Choonadi. Ndipo Mulungu wokonedwa, iwo akufuna kupulumutsidwa. Iwo akufuna kwenikweni...Iwo—sakungofuna chinachake chabe chimene chingangokhala cha kutentheka kwina, kujijirika kwina, dongosolo lina la chipembedzo, chikhulupiro china, mwambi wina umene wawonjezedwa. Iwo akumvetsa, Atate, kuti zimatengera Mawu a Mulungu angwirowo osakanizidwa. China chirichonse chidzachoka, ngakhale miyamba ndi dziko lapansi, koma Iwo sadzachoka. Ndipo ngati ife titakhala Mawu amenewo, dziko lidzachoka pansi pathupa, koma ife sitingachoke konse, chifukwa ife ndife Mawu amenewo, Mkwatibwi wa Mkwati.

²¹³ Ine ndikupempherera aliyense, kuti Inu mupereka kwa iwo, Atate, monga mwa pemphero langa lowona mtima... Ndipo pepani, Atate, chifukwa chokhala wa manjenje chotere usiku uno, kudumphira pano mochedwa, ndi—ndi pokhala wotekeseka, ndi kulankhula mawu odukaduka ndi olekezalekeza. Mwanjira ina imzake, Mzimu Woyera

wopambana, alumikizeni iwo palimodzi mwanjira Yanuyanu Yauzimu. Ndipo kawatuleni iwo ku mitima ya anthu kuchokera mu mtima wanga ndi momwe ndikuzitengera ndi zolinga zomwe ziri mu mtima wanga kwa icho. Simutero Inu, Ambuye. Ndipo pulumutsani amene angapulumutsidwe ndi kuwakokera kwa Inu, Ambuye. Ndipo ife tikhale okonzekera ora lokwatulalo lomwe posachedwa layandikira. Pakuti ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Mulungu akudalitseni. Tsopano apampando a—a
msonkhanowu. 

MKWATULO CHA65-1204
(The Rapture)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Loweruka usiku, Disembala 4, 1965, ku Ramada Inn mu Yuma, Arizona, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1993 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1993 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org